4001

# Zifanizo Za Yesu Nchito Yace



AT31
Nyanja

# JESUS' USE OF PARABLES
(Nyanja)

First Published in Zambia
The Baptist Publishing House of
the Baptist Mission of Zambia
P.O. Box 1995
LUSAKA, ZAMBIA

ZA M'KATIMU


| MUTU | | TSAMBA |
|---|---|---|
| 1 | ZIFANIZO ZA YESU, NCHITO YACE.. | 1 |
| 2 | KODI UFUMU WA MULUNGU ULI WOFANANA NDI CIANI?............ | 8 |
| 3 | NDI MTENGO WA MOYO WANGA ...... | 14 |
| 4 | KUFUNA CIKONDI KWA MULUNGU .... | 19 |
| 5 | NJIRA YOMWE MULUNGU APATSIRAMO MPHATSO....................... | 25 |
| 6 | KUPITILIRA M'PEMPHERO.......... | 30 |
| 7 | UMUNTHU PAMASO PA MULUNGU...... | 35 |
| 8 | KUDZIWA NDI KUCITA CIFUNIRO CA MULUNGU....................... | 40 |
| 9 | KODI CUMA COONA NDI CITI?...... | 46 |
| 10 | KUKHALA MU LAMULO LA CIKONDI... | 51 |
| 11 | KUKHULULUKILIDWA NDI KUKHULULU-KIRA.......................... | 56 |
| 12 | KUKONZEKERA ZA KUBWERA KWACE... | 62 |
| 13 | KUCIGWIRITSIRA NCHITO KAPENA KUCITAYA...................... | 67 |

ramo.

2. Mulungu nayenso apatsa ana ace mpata wa kumutumikira.

3. Mulungu akhala wokondwa ngati mwai womwe tinapatsidwa tiugwiritsira nchito munjira ya ubwino. Motero atipatsa zambiri, ndi kuti atipatsa mwai waukuru wa kutumikira.

4. Koma Mulungu amacotsa mwai ndi danga ku munthu yemwe safuna kugwiritsira nchito mwai wace mwa ubwino. Mpata uzapatsidwa kwa munthu yemwe azadziwa kagwiritsidwe ka nchito.



MUTU 1

# ZIFANIZO ZA YESU, NCHITO YACE

MAU A MULUNGU: Yesaya 6:9-10; Mateyu 13:1-30; 34-43

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Mateyu 13: 10-17, 34-34

MAU APAMTIMA:

*Pakuti palibe cinthu cobisika, cimene sicidzakhala coonekera; kapena cinsinsi cimene sicidzadziwika ndi kubvumbuluka. Cifukwa cace yang'anirani mamvedwe anu; pakuti kudzapatsidwa kwa iye amene ali naco; ndipo kwa iye amene alibe cidzacotsedwa, cingakhale cija aoneka ngati ali naco.*

*Luka 8:17-18*

MAU OYAMBA

Kodi fanizo ndi ciyani? Fanizo citanthauza kuti, njira ina yomwe anali kulankhulilamo mwa cisanzo kulinganiza nkhani ziwiri, zomwe zili zofanana.

Nthawi ina Yesu analinganiza Mzimu Woyera kufanana ndi mphepo yogunda. Anauza munthu kuti "Siungaone mphepo koma ungamve cabe kuomba kwace. Mzimu Woyera uli ngati mphepo."

Yesu sanali munthu woyamba kuphunzitsa ndi fanizo. Mafanizo ambiri amapezekanso mu cipangano cakale. M'modzi wa anthu ndi Yesaya 5:1-7. Uyu ananena fanizo la Munda wa m'pesa.

Yesu anadziwa kuti zinthu zomwe anafuna kuti aphunzitse anthu, sizinali zapafupi kuzimva. Motero anayamba kuuza anthu kuphyolela mu nthano motero kuti angamve comwe Yesu anali kufuna kuti awaphunzitse.

Nthawi zina Yesu anali kuyesa anthu. Nanena kuti "Kodi comwe mulingalira ndi ciyani?" Anali kufuna kudziwa kuti kodi anthu amamva

comwe akuphunziraci? Mwina anali kulankhula kuti, "Iye yemwe ali ndi makutu akumvela comwe ndilankhula amvere." (Yanganani Mateyu 11:15) Anatanthauza kuti, "ndi kuuzani cinthu comwe cili coposa nthano. Pezani tanthauzo lace loona."

## II KUMASULIRA KWA NTHANO

*10 Ndipo ophunzirawo anadza, nati kwa Iye,*
*Cifukwa canji muphiphiritsira iwo m'mafanizo?*
*11 Ndipo Iye anayankha nati, Cifukwa kwapatsi-*
*dwa kwa inu kudziwa zinsinsi za Ufumu wa*
*Kumwamba, koma sikunapatsidwa kwa iwo. 12 Paku-*
*ti yense amene ali nazo, kudzapatsidwa kwa iye,*
*ndimo adzakhala nazo zocuruka; koma yense amene*
*alibe, cingakhale comwe ali naco cidzacotsedwa*
*kwa iye. 13 Cifukwa cace ndiphiphiritsira*
*iwo m'mafanizo; cifukwa kuti akuona samaona,*
*ndi akumva samamva, kapena samadziwitsa.*
*14 Ndipo adzacitidwa kwa iwo mau adanenera*
*Yesaya, amene ati: "Pakumva mudzamva, ndipo*
*simudzazindikira konse; Pakupenya mudzapenya,*
*ndipo simudzaona konse. 15 Cifukwa unalemera*
*mtima wa anthu awa, Ndipo m'makutu ao anamva*
*mogontha, Ndipo maso ao anatsinzina; Kuti*
*asaone konse ndi maso, Asamve ndi makutu,*
*Asazindikire ndi mtima wao, Asatembenuke, Ndipo*
*ndisawaciritse iwo." 16 Koma maso anu ali*
*odala, cifukwa apenya; ndi makutu anu cifukwa*
*amva. 17 Pakuti indetu ndinena kwa inu,*
*kuti aneneri ambiri ndi anthu olungama analaka-*
*laka kupenya zimene muziona, koma sanaziona;*
*ndi kumva zimene muzimva, koma sanazimva.*

*34 Zonsezi Yesu anaziphiphiritsira*
*m'mafanizo kwa makamu a anthu; ndipo kopanda*
*fanizo sanalankhula kanthu kwa iwo; 35 Kuti*
*cikacitidwe conenedwa ndi mneneri, kuti :*
*"Ndidzatsegula pakamwa panga ndi mafanizo,*
*Ndidzaulula zinthu zobisika ciyambire kukhazi-*
*kidwa kwace kwa dziko lapansi."*

*Mateyu 13:10-17, 34-35*



Yanganani mu ndime 28 kuti mupedze comwe cidacitika kundalama zace.

Ndalama zace zinalandidwa.

## TANTHAUZO LA FANIZO

Kodi munakhalapo kale ndi mantha akucita nchito ya Ambuye Yesu? Kodi munapeza kuti tsiku ndi tsiku munali kuyesa, nchito inayamba kukupepukirani?

Mu ndime 29, Yesu anakhazikitsa coonadi, cakugwiritsira nchito ndalama. Ngati munthu agwiritsira nchito ndalama yace, izaculuka. Imagwira nchito motere: Patsiku loyamba kuti muphunzitse sande sukulu, cinali capatali kuti muciyambe. Koma cimakhala ca pafupi ngati muyesa mwa pang'ono pang'ono. Ndi cifukwa ninji? Ndikamba kakuti muphunzira pomwe mulimbikira kuyesa nchito yanu ikupita patsogolo.

Mzimai wina anamva munthu ali kuimba cilimba. Anati kwa mtsikana yemwe anali kusewela cilimba, "bwenzi ndi kadakhala ndi cifuno cako." Mzimai yemwe anali kuliza cilimba anali atakalamba kwambiri. Anati, ngati uzayamba kusewela cilimbaci tsiku ndi tsiku, kwa maola asano ndi atatu, kwa zaka makhumi asano, uzakhala ndi ukatswiri monga wanga. Ici ndicomwe Yesu anatanthauza za kukula mu zinchito. Sayembekeza cimodzi kwa munthu. Ayembekeza kalikonse ku munthu aliyense.

Mu ndime 30 imatiuza comwe cidacitika kwa kapolo waulesi. Anzace ena anali kucita zabwino nayenda munjira yabwino. Wopanda nchito wina ayenda mumdima ndi kukhala ndi mcisoni ca muyaya.

## NDEMANGA

1. Mulungu anapatsa munthu ali yense danga ndi mwai wa kumusewenzera. Sanapatse munthu aliyense njira imodzi ya kumtumiki-

Mbuye uja anaitana akapolo ace onse kwa iye. Munthu ndi munthu anali kunena zanchito yomwe anagwira ndi ndalamazo, (ndime 19). Kapolo uja yemwe anali ndi ndalama zambiri ananyamuka pamaso pa mbuyawo. Sanali ndimantha kapena kumva manyazi. Anagwiritsira nchito ndalama zambuyace munjira ya bwino. Mwacikhulupiriro anaculukitsa ndalama za mbuyace. Mbuye wace anamutamanda. Anaitana munthu uja "munthu wacikhulupiriro" Mbuye uja anapatsa udindo waukuru kwamunthu uja, kuyanganira nchito ya ikuru. Anaitana akapolo ena kuti azakondwele ndi zinthu zabwino, (ndime 21).

Tsopano mwamuma wina, yemwe anali kapolo waciwiri, yemwe anapatsidwa ndalama zokwanira zikwi khumi ndi zinai, anaima pa maso pa mfumu. Anacita cimodzi-modzi monga munthu woyamba anacita, anaculukitsa ndalama za Mbuyace. Mbuyace anamutamanda. Munthuyu cimodzimodzi momwe munthu woyamba anamucitira. Mbuye uja anamuitana kuzadya zabwino munyumba ya mbuyace.

Anthu oyamba aja anali okondwa kuona mbuyawo. Anagwiritsira nchito mphatso yao munjira ya bwino. Anakhala ndi ndalama zambiri, za mbuye wawo.

Kapolo wacitatu sanali wokondwa ku komana ndi Mbuye wace. Sanakhulupirire mbuyace. Anaitana Mbuye wace kukhala wouma mtima ndi kuti anali ndi kaweluzidwe koipa. Anati, anali ndimantha kugwiritsira nchito ndalama yace. Kodi anacita nayo bwanji ndalama ija? Welengani ndime 25.

Mwamuna uja anabisa ndalama zace pansi panthaka. Kodi Ambuyace anati bwanji kwa iye? Welengani ndime 26. Anamucha munthu wa ulesi. Anati ndalama zanga mwina ndinangoziika munyumba yosungilamo ndalama. Nyumba ya ndalama ikadandiikirapo ndalama ya kuyamika pa mwamba. Motero akanakhala ndi kandalama kang'ono kapamwamba. Koma kapolo palibe comwe anacitapo, ndikuti analibe cakumupatsa mbuyace.



FANIZO LA MSAMARIYA WACIFUNDO



A. Fanizo

Yesu anali kuphunzitsa munyumba. Anaturuka munyumba napita kumbali kwa nyanja. (Mateyu 13:1) Anthu ambiri anadza kuzamvera zomwe anali kuphunzitsa.

Yesu anakwela mungalawa nakhala pansi motero kuti aziphunzitsa anthu. Khamu la anthu linaima m'mbali mwa nyanja.

Anthu ambiri pakhamu lija anali alimi. Yesu anaphunzitsa fanizo la munthu wolima motero kuti alimi aja angamvetsetse bwino.

Mu Mateyu 13:3-9 Yesu ananena za nthano ya mulimi yemwe anabyala mbeu zace. Welengani fanizo kucokera m'Buku Lopatulika.

Yesu Kristu anati ufumu wa kumwamba uli ngati zinthu za m'munda. Mulimi ananyamuka ulendo wace wa ku kabyala mbeu. Sanabyale mbeuzo mu mizere. Anaponya mbeu zace pantaka ponse-ponse pomwe anali kuyenda m'munda mwace.

Mbeu zina zinagwà mbali mwa njira. Mbalame zinadza nazidya mbeu zija. Zina zinagwa patanthwe pouma. Ndipo zinamera mwamsanga zinafanso. Popeza zinalibe mizu. Zina zinagwa paminga. Minga inakula mwamsanga, motero mbeu zija zinalephera ku kura. Mbeu zina zinagwa panthaka yabwino. Mbeuzi zinakula ndi kukhala ndi zipatso.

B. Yankho lace

Yesu anatanthauza kuti pomwe tiuza anzathu za momwe tiza pulumutsidwila, ena sazamvera. Ena azaoneka okondwa pa kulandira Kristu. Patapita nthawi azaiwala za Mulungu. Anthuwa sanabvomere zoona Kristu kukhala mpulumutsi wao, motero alibe mphamvu zakulimbika monga mizu.

Yesu anatanthauzira kuti ena azayesa kumva



asananyamuke aitana akapolo ace atatu. Munthu uja anapatsa ndalama ku akapolo ace. Anawaika kuti azisunga nyumba ndi cuma cace.

Akapolo aja anali ndi malingalilo osiyana. Motero mbuyawo uja anapereka ndalama ku akapolo aja munthu ndi munthu anatenga ndalama zomwe zikadakwanira kugwiritsira nchito (ndime 15).

Kapolo m'modzi anapatsidwa ndalama makhumi atatu ndi asano. Munthu waciwiri anapatsidwa ndalama chikwi cimodzi ndi makhimi anai. Munthu wacitatu anapatsidwa ndalama madzana asano ndi awiri.

Mbuye wao anafuna kuti anthu aja agwiritsire nchito ndalama zija kuti apedze ndalama zambiri.

## KUGWIRITSIRA NCHITO MATALENTE

Welengani ndime 16-18 mobwezapo. Kodi ndimotani momwe anthu aja anagwiritsira nchito ndalama? Munthu uja woyamba yemwe anapatsidwa ndalama makhumi asano, anaika ndalama zace kunyumba yamalonda. (Kutanthauza kuti anacita nayo citukuko.)

Munthu woyamba uja anakweza ndalama zace kawiri, kuposa momwe anapasidwira ndi Mbuye wace. Munthu waciwiri uja nayenso anaonjeza ndalama zace kawiri kuposa momwe anampatsira mbuyace. Anagwiritsira nchito mphatso yace motero kuti apange ndalama zina.

Kodi munthu wacitatu anacita ciyani? Anali ndi ndalama zokwanira madzana asanu ndi awiri, sanagwiritsire nchito ndalamazo pezani yankho mundime 18.

## KUBWELA KWA AMBUYE WAWO

Mwini ndalama anayenda pa ulendo wapatali, motero anali atakhalako masiku ambiri-mbiri. Welengani ndime 19-30 za kubwelera kwace mu ndime 19-30.

*onani ndapindulapo ndalama zisanu zina. 21*
*Mbuye wace anati kwa iye, Cabwino, kapolo iwe*
*wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupirika*
*pa zinthu zambiri; lowa iwe m'cikondwero ca*
*mbuye wako. 22 Ndipo wa ndalama ziwiriyo ana-*
*dzanso, nati, Mbuye, munandipatsa ine ndalama*
*ziwiri; onani, ndapindulapo ndalama zina ziwiri.*
*23 Mbuye wace anati kwa iye, Cabwino, kapolo*
*iwe wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupi-*
*rika pa zinthu zing'ono, ndidzakhazika iwe pa*
*zinthu zambiri; lowe iwe m'cikondwero ca mbuye*
*wako. 24 Ndipo uyonso amene analandira ndala-*
*ma imodzi, anadza, nati, Mbuye, ndinakudziwani*
*inu kuti ndinu munthu wouma mtima, wakututa*
*kumene simunafesa, ndi wakusonkhanitsa kumene*
*simunawaza; 25 ndinaopa ine, ndinapita,*
*ndinabisa pansi ndalama yanu: onani, siyi yanu.*
*26 Koma mbuye wace anayankha, nati kwa iye,*
*Kapolo iwe woipa ndi waulesi, unadziwa kuti*
*ndimatuta kumene sindinafesa, ndi kusonkhanitsa*
*kumene sindinawaza; 27 cifukwa cace ukadapere-*
*ka ndalama zanga kwa okongola ndalama, ndipo*
*ine pobwera ndikadatenga zanga ndi phindu lace.*
*28 Cifukwa cace cotsani kwa iye ndalamayo,*
*muipatse kwa amene ali nazo ndalama khumi. 29*
*Pakuti kwa yense amene ali nazo, kudzapatsidwa,*
*ndipo iye adzakhala nazo zocuruka; koma kwa iye*
*amene alibe, kudzacotsedwa, cingakhale cimene*
*anali naco. 30 Ndipo ponyani kapoloyo wopanda*
*pace ku mdima wakunja; kumene kudzakhala kulira*
*ndi kukukuta mano.*

*Mateyu 25:14-30*

Anthu ena ali okonzeka kucita zinthu zambiri. Anthu ena ali ndi mwai waukuru wa kucita zinthu. Ena angacite zinthu zocepa cabe. Anthu ena ali ndi cizolowezi cakucita cinthu cimodzi cabe. Yesu sanatifunse kuti tiyenera kucita zinthu zomwe zili zolimba kwa ife. Afunsa ife kugwiritsa nchito mwai womwe tirinawo kuthandiza kuti nchito yace ingapite patsogolo, kukola miyoyo ya anthu, kwa iye.

Yesu anati ufumu wa kumwamba uli ngati munthu uja yemwe apita kukasaka nyama. Pomwe



kwa kanthawi kang'ono. Patapita nthawi akhoza kukokedwa ndi zinthu zina. Motero aiwala kutsatira Mulungu.

Mu nthano ya Yesu, ena anabvomera nakhala ndi cikhulupiriro. Anauzako ena momwe angapulumutsidwire. Iwo sanasiye kutsatira Mulungu. Anabala mphatso.

C. Funso

Ophunzira anamva Yesu ali kulankhula nthanoyi ya kubyala mbeu. Sanakhoze kumva zomwe anatanthauza ponena za nthanoyi. Yankho yomwe Yesu anapereka limapezedwa mu malemba athu alero omwe tiphunzira.

D Yankho la Yesu

Yesu anayankha ophunzira Mafunso awo mundime 11-13. Welengani ndime mobwezapo. Yesu anazindikira nkhope za anthu ambiri omwe anali ciimire motero analingalira za kupereka nthano zina, ndi cozizwa cina. (Anali atacilitsa munthu yemwe anali ndi dzanja lopunduka. Mateyu 12:10) Anthuwa sanafunezoona kukhala ophunzira ace. Sanafune kusintha mukhalidwe wao.

Yesu ananena cinthu cotere, "Ndifuna inu kuti mumvetsetse kuphunzitsa kwanga. Ndizakumasulilani izo kwa inu. Koma anthu ambiri ayanganira ciziwitso. Afuna kuona zozizwa. Samvera za mau omwe ali kuphunzitsidwa apa za mbiri yabwino ya ufumu wa kumwamba wa Mulungu (ndime 11). Ngati adziwa coonadi, sakakagwiritsira nchito munjira yoyenera. Anthuwa sazamvetsetsa tanthauzo la mau anga."

Yesu anafuna kuti iwo omwe afuna kumvela ndi kuphunzira, aphunzire zambiri. Kwa iwo omwe afuna kukhala osamvela sazaphunzira kanthu konse, kuzomwe Yesu anali kulankhula. Anadana ndi coonadi motero sanafune kumva zomwe Yesu anali kulankhula. Motero anthu ambiri analeka kumutsatira.

Mu ndime 14-15 Yesu anati anthuwa ali ngati anthu aja omwe analiko munthawi ya Yesaya pomwe anali mneneli. Welengani Yesaya 6:9-10 kucokera m'Buku Lopatulika lanulo.

Tsopano welengani ndime 16-17 kucokera mbuku la Mateyu 13. Yesu anali kulankhula kwa ophunzira ace. Mundime ziwirizi pedzani mau omwe Yesu anagwiritsira pa kuuza ophunzira ace.

Yesu anagwiritsira nchito liu la kuti "dalitso". Ophunzira a Yesu anali ndi mwai kapena dalitso. Anali ndi danga la kumuona iye, monga munthu. Aneneli amasiku akale anali ndi cifuno cakufuna kuti aone Yesu. Koma mwaiwo sanakhale nawo.

Tsopano ophunzira ace aja sanali kudziwa kanthu ponena za Ambuye. Anaphunzira zambiri tsiku ndi tsiku. Anali kumutsatira kamba kakuti anali kumukhulupirira m'mau ace.

Mundime 34-35, Mateyu ananena za zinjira za Yesu mkaphunzitsidwe ka kuphyolela munthano, motero anali kukwanilitsa uthenga wa Masalmo 78:2, "Ndizatsegula pakamwa panga mofunizira. Ndizachula zinsinsi zoyambira kale,"

III KUTSILIZIRA

Kwa inu

Mungamvetsetse zakaphunzitsidwe ka Yesu ngati muli aKristu. Funsani mzimu woyera kuti akuthandizeni. Azakuthandizani kudziwa tanthauzo la mau a Yesu.

NDEMANGA

1. Fanizo ndi nthano cilankhuliro, colinganiza zinthu ziwiri, mau a Mulungu ndi mkhalidwe wa umoyo wathu watsiku ndi tsiku.

2. Yesu anagwiritsira nchito nthano m'kuphunzitsa kwace. Nthano zinathandiza iwo



MUTU 13

# KUCIGWIRITSIRA NCHITO KAPENA KUCITAYA

MAU A MULUNGU: Mateyu 25:14-30

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Mateyu 25:14-30

MAU APAMTIMA:

*Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika.*

*1 Akorinto 4:2*

Nthano ya atsikana khumi, Yesu analankhula za kubwera kwace kwa ciwiri. Anauza anthu kukhala okonzekera. Ngati tikhala okonzekera, tizapulumutsidwa. Tidzakhala ndi umoyo wa ukristu. Pomwe tikhala mwa kristu, tizagwiritsira nchito khama lathu kamba ka iye.

Pomwe tiphunzira phunziroli, yanganani za mau a Yesu omwe atiuza kuti comwe tiyenera kucita ndi khama lathu lomwe anatipatsa. Welengani ndime kucokera m'Buku Lopatulika.

MAU A MULUNGU

*14 Pakuti monga munthu, wakunka ulendo,*
*aitana akapolo ace, napereka kwa iwo cuma cace.*
*15 Ndipo mmodzi anampatsa ndalama za matalente*
*zisanu, ndi wina ziwiri, ndi wina imodzi; kwa*
*iwo onse monga nzeru zao; namuka iye. 16 Pomwe-*
*po uyo amene analandira ndalama zisanu, anapita*
*kugula nazo malonda, napindulapo ndalama zina*
*zisanu. 17 Cimodzimodzinso uyo wa ziwirizo,*
*anapindulapo zina ziwiri. 18 Koma uyo amene*
*analandira imodziyo anamuka, nakumba pansi*
*naibisa ndalama ya mbuye wace. 19 Ndipo*
*itapita nthawi yaikuru, anabwera mbuye wa*
*akapolo awo, nawerengera nao pamodzi. 20 Ndipo*
*uyo amene adalandira ndalama za matalente zisa-*
*nu anadza, ali nazo ndalama zina zisanu, nanena,*
*Mbuye, munandipatsa ndalama za matalente zisanu,*

kuti alowe.

Atsikana sanayenderane ndi mwambo wa ukwati. Nyali zao sizinaikidwe mnjira yabwino. Sanali okonzeka pomwe mwini ukwati anabwela. Anali atacedwa kale.

Yesu analinganiza za kubwela kwace monga mwini ukwati. Panalibe munthu yemwe adziwa nthawi yomwe abwelelamo. Monga atsikana khumi, ena anali okonzekera; ena sanali okonzekera.

Ngati tiri okonzekera za kubwela kwa Yesu, tiyenera kuyamba ku pulumutsidwa. Tiyenera kukhala mu umoyo wacikristu. Kuunika kwathu kuzawala kuonetsa njira ya ena kuti nawo ayendemo, mkutsatira njira ya Mulungu.

ZA INU

Kodi muli okonzekera kukomana ndi Ambuye? "Ndime 13 ndicenjezo kwa inu: Khalani okonzekera, popeza simudziwa tsiku lomwe Ambuye azabwela."

NDEMANGA

1. Tsiku lina Yesu azabwela pa dziko la pansi. Anatiuza kukhala okonzeka kamba ka kubwela kwace. Tiyenera kupulumutsidwa. Tiyenera kukhala mnjira ya ukristu.

2. Ambiri azafuna kukhala okonzeka pomwe Yesu azabwela. Motero azakhala ocedwa kwambiri.

3. Tsopano ndi nthawi yokonzekera za kubwela kwa Ambuye.



omwe afuna kuphunzira kuti amvetsetse mau a Yesu bwino.

3. Nthano zili ndi tanthauzo kwa a Kristu amasiku ano. Ngati tiwelenga nthano za Yesu, Tizadziwa kukhala aKristu abwino.

MUTU 2

# KODI UFUMU WA MULUNGU ULI WOFANANA NDI CIANI?

MAU A MULUNGU: Mateyu 9:14-17; 13:31-33. 31-52; Marko 4:26-29

MAU A MULUNGU A M'PHUNZIRO LALERO: Mateyu 9:14-17; Mateyu 13:31-33; Mateyu 13:31-32; Marko 4: 26-29

MAU APAMTIMA

*Musaope, kaguru ka nkhosa inu; cifukwa Atate wanu akonda kukupatsani ufumu.*

*Luka 12:32*

Sabata latha tinaphunzira za liu lochedwa "Nthano" itanthauza kulinganiza zinthu ziwiri. Imatanthauza momwe zimalinganirana ndi kusiyana kwace. Mphunziroli tizaphunzira za nthano ya ufumu wa kumwamba. Yesu anadziwa kuti ufumu wa Mulungu uzakhala wobvuta kuti anthu aumvetsetse tanthauzo lace. Anaulinganiza ku zinthu zomwe anthu anali kudziwa bwino.

*14 Pomwepo anadza kwa Iye ophunzira ace*
*a Yohane, nati, Cifukwa ninji ife ndi Afarisi*
*tisala kudya kawiri kawiri, koma ophunzira anu*
*sasala? 15 Ndipo Yesu anati kwa iwo, Nanga*
*anyamata a nyumba ya ukwati angathe kulira*
*kodi nthawi imene mkwati akhala nao? Koma*
*adzafika masiku, pamene mkwati adzacotsedwa*
*kwa iwo, ndipo pomwepo adzasala kudya. 16 Ndipo*
*kulibe munthu aphathika cigamba ca nsaru*
*yaiwisi pa copfunda cakale; pakuti cigamba cace*
*ciomoka ku copfundaco, ndipo cicita ciboo*
*cacikuru. 17 Kapena samathira vinyo watsopano*
*m'matumba akale, akatero, matumba aphulika, ndi*
*vinyo atayika, ndi matumba aonongeka; koma*
*athira vinyo watsopano m'matumba atsopano, ndi*



Atsikana opusa asanu anazindikira za kupusa kwao. Sanali okonzekera kamba ka kukhala opanda mafuta.

Atsikana aja anazindikira kulakwa kwao. Mwini ukwati akubwela. Sanali okonzekera kukomana naye. Welengani ndime 8. Kodi akazi aja anacita bwanji tsopano?

Anali ndi lingaliro la kuti anzao azawathandiza. Akazi opusa aja anati kwa akazi ocenjera, "Tipatseniko mafuta anu kuti tithileko munyali zathu."

Kodi akazi ocenjera aja anathandiza? Welengani ndime 9.

Akazi ocenjera aja sanawathandize. Anali nawo wokwanira iwo cabe. Anawauza akazi opusa aja kuti ayenera kupita kukagula mafuta awo.

Atsikanawa anayenera kucita conse comwe angapedze mwa lingaliro lakuti akomane ndi gulu lomwe lilikubwela, motero ananyamuka nathawira ku ma Sitolo omwe anali pafupi, kuti akagule mafuta.

Kodi anacedwa mukugula mafuta? Welengani ndime 10.

Pomwe akazi anali ku masitolo kukagula mafuta. Gulu lomwe anali kudikhira linafika pamalo aja omwe anali kudikhilirapo atsikana.

Akazi ocenjera anakomana ndi guru lija nayenda pamodzi. Nyali zao zinaunika mnyumba ya mwini ukwati. Anthu oitanidwa analowa mnyumba. Khomo linatsekedwa. Panalibe munthu analoledwa kulowa pa khomo litatsekedwa. Phwando linayambidwa.

Atsikana opusa aja anabweletsa mafuta awo mocedwa. Nayamba kugogoda pa khomo la nyumba ya mwini ukwati. Kodi atsikana opusa aja anacita ciyani pambuyo pace? Yanganani ndime 11. Anapempha mwini ukwati kuti awalole

Panali cabe atsikana asanu omwe anali okonzekera. Yesu anaitana atsikanawa kukhala ocenjera. Ndicifukwa ninji anaitana atsikana awa ena asanu kuti anali opusa? Welengani ndime 2-4 mobwezapo. Atsikana ocenjera ananyamula nyali. Nyali inali kuoneka ngati kabekete kakang'ono komwe kanali ndi nsalu mukati yomwe inali yonyolowa ndi mafuta kucokera mu nyaliyo. Atsikana opusa ananyamula nyali zao, koma sananyamule mafuta ena apadera. Ndicifukwa ninji akanafuna mafuta ena?

Kodi munakhalapo kale pa phwando la ukwati? Kodi mwini ukwati anasungapo anthu ali kudikhira? Mmasiku a Yesu Mwini ukwati sanali kuyendetsa (kufulumira) mwina anali kusunga anthu ali kudikhira kwa nthawi yaitali. Akazi opusa sanadziwe nthawi yomwe adzabwelelamo. Sanali okonzekera kudikhira kwa nthawi yaitali. Analibe mafuta ena akuika munyali zao.

Welengani ndime 5-6 mobwezapo. Atsikana anakhala ali kudikhira panjira pomwe anadziwa kuti azakomana naye mwini ukwati. Panapita maola. Sanabwele. Atsikana anayamba kugona. Pomwepo onse anagona.

Pamodzi atsikana opusa ndi atsikana ocenjera anagwa mturo. Koma akazi ocenjera anali okonzekera ku komana ndi gulu lija.

Atsikana opusa anangogona ndi kuti sanalingalile kanthu konse. Mafuta omwe anali munyali zao anatha motero zinayamba kuzima. Mwamsanga zinazima.

Pakati pausiku kufuula kunamveka. "Mwini ukwati ali kubwela! bwelani muzakomane naye!" (Mateyu 25:6)

Atsikana aja anauka. Ocenjera asano aja anakoleza nyali zao ndi kuikamonso mafuta ena. Mwini ukwati akubwela. Anali okonzekera ku komana ndi gulu lija (ndime 7).



*zonse ziwiri zisungika.*

*31 Fanizo lina Iye anawafotokozera iwo, nanena, Ufumu wa Kumwamba uli wofanafana ndi kambeu kampiru, kamene anakatenga munthu, nakafesa pamunda pace; 32 kamene kakhaladi kakang'ono koposa mbeu zonse, koma katakula kali kakakuru kuposa zitsamba zonse, nukhala mtengo, kotero kuti mbalame za mlengalenga zimadza, nizibindikira mu nthambi zace. 33 Fanizo lina ananena kwa iwo; Ufumu wa Kumwamba uli wofanafana ndi cotupitsa mikate, cimene mkazi anacitenga, nacibisa m'miyeso itatu ya ufa, kufikira wonse unatupa.*

*51 Mwamvetsa zonsezi kodi? Iwo anati kwa Iye, Inde. 52 Ndipo Iye anati kwa iwo, Cifukwa cace, mlembi ali yense, wophunzitsidwa mu Ufumu wa Kumwamba, ali wofanana ndi munthu mwini banja, amene aturutsa m'cuma cace zinthu zakale ndi zatsopano.*

*26 Ndipo ananena, Ufumu wa Mulungu uli wotero, monga ngati munthu akataya mbeu panthaka; 27 nakagona ndi kuuka, usiku ndi usana, ndipo mbeu zikamera, ndi kukula, iye sadziwa umo zicitira. 28 Nthaka ibala zipatso zace yokha; uyamba mmera, zitsata ngala, pamenepo maso okhwima m'ngalamo. 29 Pakucha zipatso, pamenepo atumiza zenga, pakuti nthawi yakumweta yafika.*

*Mateyu 9:14-17, Mateyu 13:31-33, Mateyu 13:51-52, Marko 4:26-29*

## 1 KUKHALA OPANDA CAKUDYA

Tsiku lina ophunzira a Yohane m'Batizi anafunsa Yesu; Kodi ndi cifukwa ninji tikhala opanda kudya? Inu pamodzi ndi ophunzira anu sacita mwambowu wopanda cakudya.

Yohane m'Batizi anali munthu wa khama. Anali kukhala mu cipululu.

Yesu anali kukhala kudya pamodzi ndi anthu. Anakonda Yohane. Koma sanalingalira cimodzimodzi momwe Yohane analingalira.

Yesu anauza ophunzira a Yohane nthano. Anati,"panthawi ya ukwati, abwenzi a wokwatiwayo sayenda cabe popanda cakudya panthawi ija yomwe ali pamodzi." Yesu anayeselera iye mwini kukhala wokwatirayo.

Anati ophunzira ace sayenera kukhala ndi njala panthawi ino. Koma pomwe azapatukana ndi iye, atatengedwa kucosedwa pamaso pao. (Welengani ndime 15).

## II CAKALE NDI CATSOPANO

Mu ndime ya 16 ndi 17, Yesu anati palibe munthu yemwe angaike cigamba pa cobvala ca kale, kucotsa ku nsalu yatsopano. Popeza cobvala cakale cimang'ambikanso muja mumalekezero a nsalu yatsopano. Cimapanga cibowo cacikuru kuposa cakale.

Yesu anati palibe munthu yemwe angaike vinyo watsopano mu m'tsuko wakale. Madzi angwiro cinali capatali kuti apezedwe. Anthu ambiri aledzela vinyo. Vinyo unapangidwa unaikidwa muzikopa zace. Zikopazi zinali zikopa za mbuzi, zomangilila m'miyendo, ndi mkhosi, motero kuti ukhale wotsekedwa. Caka ndi caka vinyo umapangidwa ndi kuikidwa mu zikopa zatsopano. Zikopa zakale zinali zolimba. Zikhoza kuonongeka pomwe vinyo utakonzeka. Vinyo ungaonongeke.

Yesu anafuna kuti ophunzira a Yohane, pamodzi ndi a Yuda ena kuti adziwe coonadi: sanaze kuzacita kaphunzitsidwe ka m'cipangano ca kale. Ndikuti sanafune kuti iwo aphatikizepo pakaphunzitsidwe kace pa kufuna kuti atsatile malamulo a mtundu wa a Farisi.

Yesu anawauza kuti miyambo yambiri ya m'tundu wa ci Yuda siizakhala yotsatirana ndi mbili yabwino ya cisomo ca Mulungu. Mbiri



*ife ndi inu; koma makamaka mukani kwa ogulitsa malonda, mukadziguLire inu nokha. 10 Ndipo pamene iwo analikumuka kukagula, mkwati anafika; ndipo okonzekawo analowa naye pamodzi muukwati; ndipo anatseka pakhomo. 11 Koma pambuyo pace anadzanso anamwali enawo, nati, Mbuye, Mbuye, mutitsegulire ife. 12 Koma iye anayankha nati, Indetu ndinena kwa inu, sindikudziwani. 13 Cifukwa cace dikirani, pakuti simudziwa tsiku lace, kapena nthawi yace.*

*Mateyu 25:1-13*

## PHWANDO LA PAUKWATI

Mmasiku aja a Yesu, maukwati anali kucitika panthawi ya usiku. Anthu awiri anali atafunsirana kwa nyengo yokwanira miyezi khumi ndi iwiri kutanthauza caka cimodzi. Panthawi ya mwezi wotsiriza kukwaniritsa caka, mwini ukwati analingalira za kukhala ndi phwando. Pomwe phwando linakonzedwa, Anapita kukatenga mkazi wace.

Anthu oitanidwa ena anapita naye kumalo komwe kunali mkaziyo. Munthu aliyense ananyamula nyali yomwe anagwiritsira nchito mafuta. Nyali zao zinali ku unika munjira yomwe anali kuyendamo pakupita ku nyumba kwa wokwatiridwayo.

Oitanidwa ena anali kudikhira pa khomo la okwatirayo. Pomwe anamva iye ali kubwelera anthu ananyamuka kukakomana naye, anapita pamodzi kukakomana ndi mwini ukwati, pamodzi ndi anthu omwe anali kubwela pamodzi. Munthu uja analowetsa anthu onse omwe anali nawo natseka khomo la nyumba yace. Mwini ukwati sanalola enanso kuti abwele mkatimo. Angakhale munthu woitanidwa, sanaloledwe kulowa, khomo litatsekedwa kale.

## ATSIKANA KHUMI

Munthanoyi Yesu alankhula, za atsikana khumi omwe anapita kukakomana ndi eni ukwati.

MUTU 12

# KUKONZEKERA ZA KUBWERA KWACE

MAU A MULUNGU: Mateyu 25:1-13; Marko 13:28-37

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Mateyu 25:1-13

MAU APAMTIMA:

*Cifukwa cace dikirani, pakuti simudziwa tsiku lace lakufika Ambuye wanu.*

*Mateyu 24:42*

Yesu anali kuphunzitsa anthu kwa zaka zitatu. Anaphunzitsa ophunzira ace zinthu zambiri. Tsopano anadziwa kuti kwasala nthawi yocepa cabe kuti asiyane nawo pano padziko la pansi kunka kumwamba.

Anayamba kuuza ophunzira ace, kuti ayenera kupita. Anawalonjezanso kuti azabwelanso. Ambuye anafuna iwo, pamodzi ndi anzao, kuti akhale okonzekera za kubwela kwace. Ndicifukwa cace Ambuye ananena za nthano ya "atsikana khumi."

## MAU A MULUNGU

*1 Pomwepo Ufumu wa Kumwamba udzafanizidwa ndi anamwali khumi, amene anatenga nyali zao, naturuka kukakomana ndi mkwati. 2 Ndipo asanu a iwo anali opusa, ndi asanu anali ocenjera. 3 Pakuti opusawo, m'mene anatenga nyali zao, sanadzitengeranso mafuta; 4 koma anzeruwo anatenga mafuta m'nsupa zao, pamodzi ndi nyali zao. 5 Ndipo pamene mkwati anacedwa, onsewo anaodzera, nagona tulo. 6 Koma pakati pa usiku panali kupfuula, Onani, mkwati! turukani kukakomana naye. 7 Pomwepo anauka anamwali onse amenewo, nakonza nyali zao. 8 Ndipo opusa anati kwa ocenjera, Tipatseniko ena a mafuta anu; cifukwa nyali zathu zirikuzima. 9 Koma ocenjera anayankha nati, Kapena sangakwanire*



yabwino siizalowa m'makutu mwa m'tundu wa ci Yuda kamba ka miyambo yao. Kulingana ndi momwe vinyo umataikira ngati uli mcikopa ca kale. Umoyo watsopano wa ku uzimu uyenera kukhala ndi cikopa catsopano (umoyo watsopano).

## III KUKULA

Welengani Mateyu 13:31-32 mobwezapo. Yesu anagwiritsira nchito mwambi wa kambeu ka kang'ono komwe kamakula kukhala cimutengo cacikulu ku ufumu wa Mulungu.

Anthu akhala ali kuona alimi ali kubyala mbeu ya Kampiru. Mbeuyi ndi imodzi ya kambeu kakang'ono. Kambeu kanakula. Mtengo unayamba ku kula tsiku lina unakhala ngati mtengo wa ung'ono,(welengani ndime 32). Mbalame zipanga zitsa mumtengowo.

Munthanoyi Yesu anaonetsa momwe ufumu wa Mulungu uKulira mumtima mwa munthu. Paciyambi cikhulupiriro cikhala cacing'ono. Akristu atsopano sakhoza kumvetsetsa za mau omwe ali m'Buku Lopatulika. Awelenga ndi kuloweza Buku Lopatulika. Tsiku lina atsogolela mzace kuti alandile Kristu monga m'pulumutsi wace. Ufumu wa Mulungu ukula mumtima mwace. Unayamba ngati mbeu yaing'ono ya m'piru.

Nthano mu ndime 33 imatiuzanso za kukula. Yesu anati ufumu wa Mulungu uli ngati cotupitsa. Mzimai amaika cotupitsa ku ufa watiligu. Ufa uja umatupa, nuukula ndi kukhala cacikuru kamba kacotupitsa comwe capatikizidwa ku ufa uja.

Nthanoyi itanthauza kuti ufumu wa Mulungu ukula momwe mKristu akulira ndi kusintha. Auzako anzao za uKristu. Ufumu wa Mulungu upitirira kukura.

Welengani ndime 51-52. Yesu anafunsa ophunzira ace ngati anali kumva zomwe anali kuphunzitsa. Nthawi zina sanamvetsetse. Yesu anati anayembekeza iwo kuti agwiritsire nchito

coonadi kucokera ku lamulo ndi ku kaphunzitsidwe kace pa za iye.

## IV KUKURA MU CISINSI

Mu buku la Marko 4:26-29, Yesu anati ufumu wa kumwamba uli ngati munthu yemwe afesa mbeu napita kukagona m'mawa mwace apeza kuti mbeu yakula. Popanda iye kudziwa comwe cacitika ku mbeu ija usiku. Tsiku lina nthawi ya ku kolola tiligu yafika.

Pomwe tiuza anthu za Kristu, cili ngati munthu yemwe afesa mbeu. Sitingapulumutse aliyense. Mulungu yekha ndiye angacite tero. Tiuza munthu momwe angapulumutsidwire. Tsiku lina munthu uja alandira Kristu. Ayamba kuwelenga Buku Lopatulika. Sitidziwa momwe cinacitikira. Koma tidziwa za ufumu wa Mulungu kuti uli kukula mumtima mwa munthu.

## V NDEMANGA

A. Tilowa mu ufumu wa Mulungu kuphyolera mucikhulupiriro mwa Yesu Kristu. Yesu Kristu yekha ndiye angapange munthu kuti akhale wobadwa mwa tsopano.

B. Pomwe Kristu apulumutsa iye, M'zimu unasintha mitima yathu.

C. Akristu atsopano apemphera Mulungu mu Chalichi. Awelenga Buku Lopatulika. Auzako ena m'mene angapulumutsidwile.

## VI NDIME YA INU

Kodi mufuna kutamandidwa pa nchito yomwe mucita panyumba? Kapena pa Chalichi yanu?

Sabata lino citani nchito ya Mulungu ndi kuti musauze munthu aliyense, momwe mwacitira nchito yanu?

A. Akristu ayenera kukagwira nchito ya Mulungu kamba kakuti amukonda, kosati



safuna kukhulululukira ena.

3. Tiyenera kukhulululukira oticimwira ife ngati tifuna Mulungu kuti atikhulululukire.

munthu uja. (ndime 30-31)

Mfumu ija inaïtana kapolo wace pamaso pace. Nthawi yomweyo mfumu anali wokwiya kwambiri. Welengani ndime 32-33 mobwezapo.

Mfumu inaitana kapolo uja kuti anali munthu wopanda cifundo, munthu woipitsitsa. Ndicifukwa ninji? Kapolo sanakhululukire ena. Mfumu inamuuza iye, ndinakhululukira iwe, nkhongole ya ndalama zonse, koma tsopano iwe siufuna kukhululukira mzako. Uyenera kukhala ndi cifundo kwa bwenzi lako."

Motero mfumu inalingalira kuti apatse cilango munthu uja kulingana ndi momwe anacitira iye kwabwenzi lace lija.

Mfumu inaponya munthu uja munyumba yandende kufikira atalipira nkhongole yonse ku mfumu.

Mu ndime 35, Yesu analonjeza ophunzira ace. Anati Mulungu azalanga iwo ngati sakhululukira anzao.

ZA INU

Yesu ananena nthano mwa kufuna kuonetsa za ku khululukira kwa Mulungu, kwa ife.

Monga kapolo uja, sitingalipire nkhongole yathu kwa Yesu popeza ndi yaikuru. Anapereka moyo wace pa mtanda kamba ka kuombola miyoyo yathu kumacimo. Azatikhululukira ngati tifunsa iye kuti atero. Mulungu ayembekeza kuti tikhululukire anzathu.

NDEMANGA

1. Mulungu atikhululukira ife pa nthawi iliyonse yomwe tingafunsiremo cikhululukiro. Afunanso a Kristu kuti akhululukire abwenzi awo.

2. Anthu ena afuna kukhululukiridwa, koma



kulingalira za kulipilidwa, kapena kutamandidwa kamba kakucita nchito yabwino.

B. Ngati pali iwo omwe mugwira nchito nawo pamodzi omwe ali olemekezedwa, tiyenera kukhala okondwa. Palibe mkristu yemwe ayenera kukhala ndi kaduka pomwe Mulungu abwela kwa anzace.

C Tiyeni tikhale oyamika pakudziwa kuti Mulungu sazapeleka mphatso kamba kazinthu zabwino zomwe timucitira. Mulungu kuphyolela mu cifundo cace azadalitsa ife tonse mosiyana-siyana.

MUTU 3

## NDI MTENGO WA MOYO WANGA

MAU A MULUNGU: Mateyu 13:44-50;
Luka 14:15-24

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Mateyu 13:44-46, Luka 14:24

MAU APAMTIMA:

*Cifukwa cace tsono, yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga.*

*Luka 14:33*

Kodi munalingalilapo kale pa za kupereka moyo wanu pa cinthu comwe mukonda? Panthawi ya nkhondo, anthu omwe ali asilikali, amapereka moyo wao kamba ka dziko lao. Bambo ndi mai angapereke moyo wao kamba ka mwana wao.

Pomwe muli kuwelenga ndi kuphunzira phunziroli, lingalirani ngati mungapereke umoyo wanu kamba ka kuti tiombole anthu anzathu kukhala a Kristu.

MAU A MULUNGU

*44 Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi cuma cobisika m'munda; cimene munthu anacipeza, nacibisa; ndipo m'kucikonda kwace acoka, nagulitsa zonse ali nazo, nagula munda umenewu.*
*45 Ndiponso Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi munthu wa malonda, wakufuna ngale zabwino: 46*
*ndipo m'mene anaipeza ngale imodzi ya mtengo wapatari, anapita, nagulitsa zonse anali nazo, naigula imeneyo.*

*15 Ndipo pamene wina wa iwo akuseama pacakudya pamodzi ndi Iye anamva izi, anati kwa Iye, Wodala iye amene adzadya mkate mu Ufumu wa Mulungu. 16 Koma anati kwa iye, Munthu wina anakonza phwando lalikuru; naitana anthu ambiri.*



Mfumu inadziwa kuti munthuyu sazakwanitsa kupereka ngongole. Anakweleta ndalama zambiri mbiri. Koma mfumu inali ndi mtima wacifundo kwambiri. (1) Anamva cisoni kamba ka kapolo; (2) Anamukhulululukira ngongole yace; (3) Anamasula kapolo uja.

Mfumu inaleka kuti kapolo uja apite. Sanalembe za nkhongole yace, nafafaniza kuti "Walipira ndalama zonse"

Kapolo uja tsopano ayenera kukhala wokonzekera kukhululukira amangawa ace nayenso. Kapolo uja sanafune kukhululukira. Welengani ndime 28 mobwezapo. Ndiciyani comwe anacita? Anakomana ndi munthu yemwe anali kugwira nchito naye pamodzi. Munthu uja anali atakongola ndalama za zing'ono kwa munthu wokhulukiridwa uja. Munthu woyamba uja yemwe anakongolela mfumu ndalama zambiri-mbiri.

Kodi munthu uja anayembekezera munthu uja yemwe anali ndi nkhongole yace kuti apite kukatenga ndalama? Iai. Anagwira bwenzi lace pakhosi. Anati, "lipira ndalama zanga zomwe unatenga."

Kodi ndime 26 ndi ndime 29 ziribwanji apa?

Mu ndime 26 munthu woyamba anapempha cikhulululukiro. Analonjeza kuti azalipira ndalama ija yomwe sakanatha kuilipira. Anafuna kukhulukilidwa koma iye sanali kufuna kukhulukira ena.

Mu ndime 29, munthu wa ciwiri uja anapempha cikhulululukiro. Analonjeza kuti azalipira nkhongole yace yomwe inali ya ing'ono. Munthu woyamba uja sakanatha kukhulululukira munthu uja.

Kodi munthu woyamba anacita ciyani? Anamangitsa bwenzi lace naponyedwa m'ndende. Akapolo ena, anamva za ici. Anadziwa kuti munthuyo ndi yemwe anakhulululukiridwa kwa mfumu, anali ndi nkhongole yaikuru, kapolo wina ananyamuka nakauza mfumu comwe cinacitika ku

cabe kunali kukhululukira kwa kukuru kwa ocimwayo. Welengani ndime 22.

Yesu anamuyankha kuti sikukhulukira munthu paciwelengero ca kasano ndi kawiri, koma makhumi asano ndi awiri kukwaniritsanso motero, kutanthauza (madzana anai ndi makhumi asano ndi awiri.)

Yesu anatanthauza kuti musaleke kukhululukira muyenera kupitilizapo ku khululukira amangawa athu. Anadziwa kuti anthu anafunsa Mulungu kuti awakhulukire, koma munthu sakhululukira mnzace. Yesu ananena za nthano ya munthu yemwe anali kapolo wosakhulupirika, yemwe anaonetsa zakukhala wopanda cifundo pa mzace. Welengani ndime 23-24 mobwezapo.

Yesu ananena kuti ufumu wa kumwamba unali ngati ufumu wa padziko la pansi. M'fumu inaitana akapolo ace kwa iye. Akapolowa anali ndi ndalama za mfumu. M'fumu inafuna kuyangana za ciwelengero ca ndalama zace. Anali kufuna kudziwa ngati ndalama zace zonse zinalipo.

Ndalama zina zinali kusowa. Kapolo wina anabweleka ndalama zambiri. Anali ndi nkhongole ya ndalama zambiri kwa mfumu (madzana makhumi asanu).

Mnthawi ya Yesu munthu anali kugulitsidwa mu ukapolo ngati, munthu uja anali ndi nkhongole ya ndalama zambiri, motero kuti abwezere nkhongole. Munthu sakanatha kulipira ndalama zonse zomwe anakongola kwa mfumu. Welengani ndime 25 muone comwe mfumu inacita.

Mfumu inauza akapolo ace ena kuti ayenera kugulitsa munthu wa nkhongole uja pamodzi ndi banja lace, ndi zonse zomwe anali nazo.

Kodi kapolo anali ndi mantha? Ndi ciyani comwe anacita? Yanganani ndime 26.

Kapolo uja anapempha cikhululukiro. Analonjeza kuti azapereka nkhongole.



*17 Ndipo anatumiza kapolo wace pa nthawi ya*
*phwando kukanena kwa oitanidwawo, Idzani, cifu-*
*kwa zonse zakonzeka tsopano. 18 Ndipo onse*
*ndi mtima umodzi anayamba kuwiringula. Woyamba*
*anati kwa iye, Ine ndagula munda, ndipo ndiyene-*
*ra ndituruke kukauona; ndikupempha undilole ine*
*ndisafika. 19 Ndipo anati wina, Ine ndagula*
*ng'ombe za magori asanu, ndipo ndinka kukaziyesa*
*ndikupempha undilole ine ndisafika. 20 Ndipo*
*anati wina, Ine ndakwatira mkazi, ndipo cifukwa*
*cace sindingathe kudza. 21 Ndipo kapoloyo pa-*
*kubwera anauza mbuye wace zinthu izi. Pamenepo*
*mwini nyumba anakwiya, nati kwa kapolo wace,*
*Turuka msanga, pita kumakwalala ndi ku njira*
*za mudzi, nubwere nao muno aumphawi ndi opundu-*
*ka ndi akhungu ndi otsimphina. 22 Ndipo kapolo-*
*yo anati, Ambuye, cimene munacilamulira*
*cacitika, ndipo malo atsalapo. 23 Ndipo mbuye*
*ananena kwa kapoloyo, Turuka, nupite kumiseu*
*ndi njira za kuminda, nuwaumirize anthu alowe,*
*kuti nyumba yanga idzale. 24 Pakuti ndinena*
*kwa inu, kuti kulibe mmodzi wa amuna oitanidwa*
*aja adzalawa phwando langa.*

*Mateyu 13:44-46, Luka 14:15-24*

Mtundu wa ci Yuda unali kuika cuma ca golide pansi. Sanali kuika m'nyumba zao ai. Mwa ici mwina munthu uja anali kufa popanda kuuza anthu komwe kunali cuma cace. Patapita zaka zambiri mwina anthu aja anali kupeza cuma ca wakufayo. Motero a Yuda ambiri anali ndi nthawi ya kufuna funa komwe angapedze cuma ca golide.

Yesu analinganiza ufumu wa kumwamba, ndi golide womwe munthu anapedza (Mateyu 13:44). Anali kuufuna kwambiri. Kodi ndi ciyani comwe anacita?

Munthu uja angulitsa zonse zomwe anali nazo nagula munda! Kodi ici cingakhale ca cilendo lelo?

Yesu anali kulankhula kuti munthuyu wapedza ufumu wa ku mwamba. Anaphunzira momwe

angakhalire mkristu. Anaphunzira nadziwa bwino tanthauzo la kukhala mkristu. Anaona mtengo wa kukhala mkristu. Ali ndi cifuno cakukhala kapena kuzipereka moyo wace kamba ka Kristu.

Welengani Ndime 45-46 mobwezapo. Mnthano-yi Yesu akali kulankhula za ufumu wa kumwamba. Golide khumi, inali ngati ndi cuma ca masiku ano. Munthu anali ku funa-funa golide yabwino.

Pomwe munthu asanapulumutsidwe, ali ngati munthu uja yemwe afuna-funa golide yabwino. Anthu ambiri akhala zaka zambiri kwa mbiri asanapedze Kristu. Afuna-funa iye m'malo ambiri, ngakhale m'machalichi. Nthawi zina akhristu akhala osokonezeka pakufuna komwe angapedze Kristu . Ena amalingalira kuti ngati apita ku Chalichi nalowa mujamo ndi momwe angapedze Kristu. Anthu ambiri samamvera bwino kuti "Ocimwa apulumutsidwa kuphyolela mucikhulupiriro." Pomwe wina alandira Yesu Kristu kukhala mphulumutsi wace, iyeyo apedza mtendere momwemo.

Yesu anati pomwe munthu adziwa zakukoma kwace kwakukhala mkristu, angakhale nalo danga la kutsatira Kristu.

## PHWANDO LALIKURU

Mu Luka 14:1 imati, "Ndipo panali pamene Iye analowa mnyumba ya m'modzi wa akulu a Afarisi tsiku la Sabata, kukadya, iwo anali kumzonda iye."

Afarisi anali a mtundu wonyada. Pomwe anakhala pansi kuti adye, Yesu anawaona ali kusankha malo abwino a kuti iwo akhalepo. Yesu anafuna iwo kuti alingalire za anzao naonso. Anakambilana nawo amuna aja za umunthu. Motero anawauza za nthano.

Welengani buku la Luka 14:15-24 ponena za Phwando lalikuru. Yesu anati munthu anapatsa



*anasowa kanthu kombwezera, mbuye wace analamulira kuti iye agulitsidwe, ndi mkazi wace ndi ana ace omwe ndi zonse ali nazo, kuti akabwezedwe mangawawo. 26 Cifukwa cace kapoloyo anagwada pansi, nampembedzera, nati, Mbuye, bakandiyembekezani ine, ndipo zonse ndidzazibwezera kwa inu. 27 Ndipo mbuye wa kapoloyo anagwidwa ndi cisoni mumtima, nammasula iye, namkhululukira ngongole. 28 Koma kapolo uyu, poturuka anapeza wina wa akapolo anzace yemwe anamkongola iye marupiya atheka makumi khumi, namgwira, namkanyanga pakhosi, nati, Bwezera cija unacikongola. 29 Pamenepo kapolo mnzaceyu anagwada pansi, nampempha iye, nati, Bakandiyembekeza ine, ndipo ndidzakubwezera. 30 Ndipo iye sanafuna; koma anamuka, namponya iye m'nyumba yandende, kufikira abwezere ngongole. 31 Cifukwa cace m'mene akapolo anzace anaona zocitidwazo, anagwidwa cisoni cacikuru, nadza, nalongosolera mbuye wao zonse zimene zinacitidwa. 32 Pomwepo mbuye wace anamuitana iye, nanena naye, Kapolo iwe woipa, ndinakukhululukira iwe mangawa onse aja momwe muja unandipempha ine; 33 kodi iwenso sukadamcitira kapolo mnzako cisoni, monga inenso ndinakucitira iwe cisoni? 34 Ndipo mbuye wace anakwiya, nampereka kwa azunzi, kufikira akambwezere iye mangawa onse. 35 Comweconso Atate wanga adzacitira inu, ngati inu simukhululukira yense mbale wace ndi mitima yanu.*

*Mateyu 18:21-35*

## FUNSO LA PETRO

Petro anali myuda. Ayuda ena anali kuti munthu ayenera kukhulukira mnzace atalakwa, katatu, pacimo limodzi. Ena anali kuti muyenera kukhulululukira mnzanu, ngati abwezapo kasano ndi kawiri. Petro anakhala odabwa pakuti sanadziwe comwe angatsatirepo monga ophunzira. Anafunsa Yesu, "Ambuye ndikangati komwe ndizakhulululukira mbale wanga yemwe andicimwira? Kasano ndi Kawiri?" Mateyu 18:21

Yesu anayankha Petro wodabwitsidwa uja. Ophunzira analingalira kuti kasano ndi kawiri

MUTU 11

## KUKHULULUKILIDWA NDI KUKHULULUKIRA

MAU A MULUNGU: Mateyu 6:9-15; 18:21-35

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Luka 10:25-27

MAU APAMTIMA:

*Ndipo mutikhululukire mangawa athu monga ifenso tikhululukira amangawa athu.*

*Mateyu 6:12*

Nthano ya phunziro la Sabata latha linatiphunzitsa za cikondi Yesu anati anthu ayenera kukonda abale awo. Nthanoyi imati tiyenera kukhala ndi mtima wacikhululukiro. Tiyenera kukhululukira ena ngati, tifuna kuti tikhululukilidwe. Kukhulukira citanthauza kuti kuiwala coipa comwe waticitira m'bale wathu. Sitiyenera kuzilingalira izo, ngati zapita, zapita. Iyi ndiyo njira yomwe Ambuye amakhululukiramo ife.

Ophunzira aja sanamvetse zatanthauzo la nthano yomwe anaphunzitsa. Tsiku lina Petro anafunsa funso ponena za ici. Welengani comwe anafunsa. Welengani nthano Yesu ananena kuyankho la Petro kuphyolera mnthano.

MAU AMULUNGU

*21 Pamene Petro anadza, nati kwa Iye. Ambuye, mbale wanga adzandilakwira kangati, ndipo ine ndidzamkhululukira iye? kufikira kasanu ndi kawiri kodi? 22 Yesu ananena kwa iye, Sindinena kwa iwe kufikira kasanu ndi kawiri, koma kufikira makumi asanu ndi awiri kubwerezedwa kasanu ndi kawiri. 23 Cifukwa cace, Ufumu wa Kumwamba ufanizidwa ndi munthu, mfumu, amene anafuna kuwerengera nao akapolo ace. 24 Ndipo pamene anayamba kuwerengera, anadza kwa iye ndi wina wamangawa wa ndalama za matalente zikwi khumi. 25 Koma popeza iye*



cakudya. Anaitana anthu ambiri. Munthu uja anaitana kapolo wace kuti abweletse anthu munyumba. M'modzi ndi m'modzi anthu aja anayamba kufunsa cikhululukiro. Welengani zomwe anthuwa ananena mundime 18-20.

Munthu woyamba anati, "Ndacoka mkugula munda. Motero ndiyenera kupita ku kauwona. Conde ndikhululukireni nthawi ino. Munthuyu sanagwiritsire lamulo labwino. Anagula munda koma sanapite kukauona coyamba.

Welengani ndime 9 muzamva madandaulo omwe anapereka ena pakufuna kukhululukilidwa.

Mundime 20 munthuyu mwina analingalira kuti iye ndiye ali ndi dandaulo labwino kuposa ena onse. Kodi anakamba ciyani munthuyu? Anati ndikamba cifukwa cakuti anali ndi mkazi watsopano. Anagwa mucikondi. Analibe cifuno ca kukapembeza Mulungu. Ufumu wa kumwamba unamuonekera kutali m'malingaliro ace. Kapolo anabwelela ndi uthenga. Panalibe yemwe anabwela kuzadya cakudya. Mfumu ija inakhala yokwiya. Anali atakonza phwando lalikuru. Anthu omwe analola kuitanidwa sanabwele.

Azibusa ambiri ndi mamembala m'machalichi amayendera anthu m'zinyumba zao mkati mwa Sabata. Anaitana anthu kuti abwele ku Chalichi. Anthu amapanga madandaulo ambiri. Ananena kuti, ndiyenera kugwira nchito Sabata lonse. Motero patsiku la Sabata ndiyenera kukhala panyumba cabe, kapena ndiyenera kuyendera makolo anga ndilibe nthawi ya kupita ku Chalichi. Zinthu zomwe afuna kucita zinali zazikuru kuposa nchito za Mulungu, ndi ufumu wace.

Munthu uja anatumanso kapolo wace kaciwiri. Welengani Luka 14:21-23 kuti akapedze anthu ena omwe sanaitanidwe paciyambi kuzadya cakudya ca m'madzulo cija.

Pomwe Yesu anali kulankhula za nthanoyi anali kutanthauza kuti Mulungu anakonza phwando

Anatuma aneneli ace anasankha oitanidwa ace, a Yuda. Anati azabwele pomwe Mulungu anatuma mwana wace, kuti abweletse oitanidwa aja ku phwando. Anthu osankhidwa ace sanabwele. Motero Mulungu anatuma mwana wace kuti abweletse munthu aliyense yemwe azapezeka.

Mulungu aitana anthu kuti abwele mu ufumu wace. Motero Ambuye anafunsa aliyense kuti abwele. Malo aliko ambiri a anthu ena. Nthawi zonse kuli malo okwanira anthu onse.

NDEMANGA

1. Cipulumutso cili ngati ndi cuma ca golide comwe cili cobisidwa. Munthu mwamwai wapeza golide ija. Pomwe munthu apedza golide, akhala ndi cimwemwe cacikuru. Cimakhala cinthu cacikuru kwambiri mu umoyo wace.

2. Anthu sakhala okondwa popanda Mulungu. Ena azafuna-funa kufikira atampedza. Apedza mtendere mwa Kristu nakhala ndi moyo watsopano.

3. Anthu ena amamva zakuitana kwa Mulungu. koma pemphani cikhulululukiro, kamba ka kusacita nchito yace. Anthuwa sazalowa ufumu wa kumwamba.



wina.

Msamariya anali ndi funso limodzi cabe: "Kodi ndi ngamthandize mnjira yotani munthu uyu?" Anacitira munthu uja monga anafunira kuti ena amcitire. Msamariya anakhala mlamulo la cikondi. Anaonetsa cikondi ku mnansi wace.

NDEMANGA

1. Buku Lopatulika linena kuti tiyenera kukonda anansi athu monga tizikondela ife eni.

2. Ngati tifunsa kuti anansi anthu ndani, sitimvetsetsa za cikondi ca Mulungu kwa anthu onse.

3. Anansi ndi anthu amene afuna thandizo. Angakhale oipa kapena abwino, olemela kapena osauka, anthu amitundu yonse. Ngati tikhala mlamulo la cikondi tizathandiza aliyense amene afuna thandizo lathu.

bwitsa wacilamulo. Yesu anati Msamariya anapitila njirayo. Awa anali anthu a mwazi wosakanizana. Anali Ayuda mbali ina ndiponso ina mbali Ahelene. Aja omwe anali Ayuda oyenera analibe nchito nawo anthu aja.

Samariya dzikoli linakomana ndi nthaka ya Ayuda. Ici cinawapanga iwo kukhala anansi awo. Ayuda sanaone a Samariya monga anansi.

Werengani ndime 33 ndi 34 kuphunzira zomwe Msamariya anacita. Pamene msamariya anaona munthu ali gone panjira, anamva cisoni. Anaika mankhwala pa zilonda zace. Anamanga pa zilondazo ndi nsaru pomwe anamva kuwawa. Tsono Msamariya anamtenga munthu uja pa bulu wace. Nadza naye ku nyumba ya alendo. Anamsamala munthu uja usikuwo.

Mmawa mwace Msamariya anapita. Werengani ndime 35 kupeza zomwe anacitira munthu uja wopwetekedwa.

Msamariya anapereka ndalama kwa mkuru wa nyumba ya alendo. Ndalamayi inali yakuthandiza kusunga munthu uja. Analonjeza kupereka ndalama zina ngati zinali kufunika, pa kubwerera.

Yesu anasiliza fanizo lace ndi funso. "Uti wa awa atatu, uyesa iwe, anakhala mnansi wa iye uja adagwa m'manja a acifwamba?" (ndime 36).

Wacilamulo anadziwa yankho. Koma sanafune kuti anene kuti ndi Msamariya. Kodi ananena ciani? Wacilamulo uja anati, "Iye wakumcitira cifundo." (Ndime 37).

TANTHAUZO LA FANIZO

Yesu anati kwa munthu uja, "Pita, nucite iwe momwemo." Tiyeni tiganizire comwe Yesu anatanthauza. Msamariya sanadziwe ngati munthu wopwetekayo anali wolemela kapena wosauka. Kunalibe kanthu ngakhale kuti anali wa mtundu



MUTU 4

## KUFUNA CIKONDI KWA MULUNGU

MAU A MULUNGU: Luka 15

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Luka 15:11-24

MAU APAMTIMA:

*Pakuti mwana wa Mulungu anadza ndi kufuna funa ndi kupulumutsa cotaikaco.*

*Luka 19:10*

Kufuna funa kutanthauza kuti kufuna cotaika. "Mulungu afuna cikondi" citanthauza kuti Mulungu afunafuna ife. Atilandira ife pomwe tidza kwa iye.

Cikondi ca Mai citithandiza ife kuti timvetsetse za cikondi ca Mulungu.

Tsiku lina mwana wa zaka zitatu anathawa pakhomo pa bambo wace. Amai a mwana uja anacita mantha. Anadziwa kuti mwina mwana uja ndi kupwetekedwa. Anamfuna funa. Koma patapita kanthawi anaona mwana uja ali kubwela. Mwana uja anali kuyenda yenda m'munda. Miyendo yace inali kuturuka magazi ndi kuti inali yotupa kamba ka minga yomwe inalasa mwana uja. Anali kulira kwambiri mwana uja "Kunena ndili wacisoni. Sindizathawathawanso kaciwiri." Amai ace popedza akonda mwana wace uja, anamukhulukira.

Mphunziroli tiphunzira nthano inanso yomwe Yesu analankhula. Yesu analankhulanso za cikondi ca Bambo wace kuti athandize a Yuda kuti amvetsetse za cikondi ca Mulungu.

MAU A MULUNGU

*11 Ndipo Iye anati, Munthu wina anali ndi ana awiri; 12 Ndipo wamng'onoyo anati kwa*

*atate wace,"Atate, ndigawirenitu zanga za pa*
*cuma canu." Ndipo iye anawagawira za moyo wace.*
*13 Ndipo pakupita masiku owerengeka mwana*
*wamng'onoyo anasonkhanitsa zonse, napita ulendo*
*wace ku dziko lakutari; ndipo komweko anamwaza*
*cuma cace ndi makhalidwe a citayiko. 14 Ndipo*
*pamene anatha zace zonse, panakhala njala*
*yaikuru m'dziko muja, ndipo iye anayamba kusowa.*
*15 Ndipo anamuka nadziphatikiza kwa mfulu*
*imodzi ya dziko lija; ndipo uyu anamtumiza*
*kubusa kwace kukaweta nkhumba. 16 Ndipo anala*
*kalaka kukhutitsa mimba yace ndi makoko amene*
*nkhumba zimadya, ndipo palibe munthu anamninkha*
*kanthu. 17 Koma m'mene anakumbukila mumtima,*
*anati,"Anchito olipidwa ambiri a atate wanga*
*ali naco cakudya cocuruka, ndipo ine ndiononge-*
*ke kuno ndi njala? 18 Ndidzanyamuka ndipite*
*kwa atate wanga, ndipo ndidzanena naye, Atate,*
*ndinacimwira Kumwamba ndi pamaso panu; 19*
*sindiyeneranso konse kuchulidwa mwana wanu;*
*mundiyese ine ngati mmodzi wa anchito anu."*
*20 Ndipo iye ananyamuka, nadza kwa atate wace.*
*Koma pakudza iye kutali, atate wace anamuona,*
*nagwidwa cifundo, nathamanga, namkupatira*
*pakhosi pace, napsompsonetsa. 21 Ndipo mwana-*
*yo anati kwa iye,"Atate ndinacimwira Kumwamba*
*ndi pamaso panu, sindiyeneranso konse kuchuli-*
*dwa mwana wanu." 22 Koma atateyo ananena kwa*
*akapolo ace,"Turutsani msanga mwinjiro wokome-*
*tsetsa, nimumbveke; ndipo mpatseni mphete ku*
*dzanja lace ndi nsapato ku mapazi ace; 23 ndipo*
*idzani naye mwana wa ng'ombe wonenepa, mumuphe,*
*ndipo tidye, tisekere; 24 cifukwa mwana wanga*
*uyu anali wakufa, ndipo akhalanso wamoyo; anali*
*wotayika, ndipo wapezedwa." Ndipo anayamba*
*kusekera.*

*Luka 15:11-24*

Nthanoyi ndiya "Mwana wotaika". Mwana wotaika anali mwana wa m'ng'ono pa awiriwa. Anali kufuna zinthu zina. Kodi ndi ciyani comwe anali kufuna? Welengani ndime 12.

Anali kufuna kuti apatsidwe gawo la cuma cace. Kodi bambo wace anacita ciyani?



ankanakhala ndi moyo wosatha.

## FUNSO LINA

Mau awa aoneka kuti munthu uja anabvutika nawo. Anakhulupilira kuti anakonda Mulungu. Sanali woona kuti mnansi wace anali ndani. Conco anafunsa funso lina. "Kodi mnansi wanga ndani?" Onani ndime 29.

Ambuye Yesu sanayankhenso funso la munthu uja. Nthawi iyi analankhula kwa iye mfanizo.

## MUNTHU ANAYENDA

Munthu wina anapita ku Yeriko kucokera ku Yerusalemu (ndime 30). Mtunda unali wa mailosi 20. Mseu uyu anapita mkati ndi kunja kwa maphiri.

Maphiri anali ndi zigwa zambiri. Acifwamba anakhala mzigwa zimenezi. Acifwamba awa anatenga ndalama ndi zinthu zina kucokera kwa anthu amene anali kuyenda ndi njirayo.

Munthu anali kuyenda m'njira iyi. Acifwamba anam'menya ndipo anatenga zobvala zace. Anasiya munthu uja pafupi ndi kufa.

Mwamsanga wansembe anapitira njirayo. Wansembe anali munthu wacipembezo amene anagwira nchito mchalichi. Anatsogolera mapemphero mkacisi. Anadziwa lamulo la kukonda mnansi. Werengani ndime 32. Kodi wansembe anacita ciani pamene anaona munthu uja atagona ali pafupi ndi kufa pa njira paja? Iye anapitira kumbali kwa njira ina.

Munthu wina anafika (ndime 32). Anali Mlevi. Alevi anathandiza ansembe kutsogolera mapemphero mkacisi. Mlevi anadziwa lamulo la kukonda mnansi wace. Kodi anacita ciani? Mlevi "anabwera pali iye ndipo anapitilila mbali ina." (ndime 32)

Mau enanso a Yesu (ndime 33) ayenera kuda-

*nadza kwa iye, namanga mabala ace, nathirapo mafuta ndi vinyo; ndipo anamuika iye pa nyama yace ya iye yekha, nadza naye ku nyumba ya alendo, namsungira. 35 Ndipo m'mawa mwace anaturutsa marupiya atheka awiri napatsa mwini nyumba ya alendo, nati, Msungire iye, ndipo ciri conse umpatsa koposa, ine pobwera, ndidzakubwezera iwe. 36 Uti wa awa atatu, uyesa iwe, anakhala mnansi wa iye adagwa m'manja a acifwamba?" 37 Ndipo anati, "Iye wakumcitira cifundo." Ndipo Yesu anati kwa iye, "Pita, nucite iwe momwemo."*

FUNSO

Ambiri anakhulupilira kuti Yesu anali mwana wa Mulungu. Anakhulupilira ziphunzitso zace. Anthu awa anayesa kunyenga Ambuye. Anayesa kuti Yesu anali mphunzitsi wa boza.

Tsiku lina wa lamulo anafunsa Yesu mafunso awiri. Anali m'modzi wa anthu amene anafuna kunyenga Ambuye.

Wacilamulo anafunsa, "Mphunzitsi, ndi zalowa moyo wosatha ndi kucita ciani?" Yesu anadziwa kuti wacilamulo anali kumuyesa iye. Munthu uja anaphunzitsa lamulo la Mose. Lamulo la Mose linali kulankhula m'mene anthu ayenera kukhalira. Munthu uja anadziwa lamulo mu mtima wace. Anadziwa kuti ayenera kucita.

YANKHO LA YESU

Yesu sanayankhe munthu uja. Anamfunsa funso. Welengani ndime 26. Wacilamulo anayankha mwamsanga. Werengani ndime 27. Wacilamulo uja anaika pamodzi la kukonda Mulungu ndi lakukonda mnansi.

Yesu anati munthu uja anayankha bwino (ndime 28). Yesu anadziwa kuti cinali capafupi kuphunzira lamulo. Anadziwa kuti cinali colimba kukhala monga lamulo linaphunzitsira. Anauza munthu uja kutsatira lamulo. Ngati anakonda Mulungu coyamba, ndi kukonda mnansi wace,



Anapatsa mwana wace uja cuma cace.

Kodi mnyamata uja anakhala okondwa pomwe analandira katundu wace? Welengani ndime 13 mumve comwe cinacitika. Kodi mwapedza kuti munthu uja anasiya nyumba ya bambo wace?

Bambo anali ndi cisoni pakuona kuti mwana uja anasiyana ndi makolo ace. M'nyamata uja anafuna kuti apite kukasewela. Anali kufuna kupita ku nyumba ya tsopano yakutali ndi mudzi wa kwao.

Welengani ndime 13 kuti mupedze komwe mwana uja anapita. Kodi anacita ciyani ndi ndalama zace? Kodi anagwiritsira nchito ciyani?

Pomwe tisanakambe zambiri ponena za mwana, tiyeni tizifunse ife eni: Kodi nthawi zonse timagwiritsira nchito nthawi yathu munjira yabwino?

BVUTO

Mwana uja anagwiritsira nchito ndalama yace zonse munjira yosayenera. Ndimkhalidwe wace unali wosayenera. Cuma nthawi zonse cibweletsa mabvuto. Mnyamata uja sanalingalire za kukhala ndi cisoni kapena kukhala m'mabvuto, kufikira pomwe anapedza kuti ali m'mabvuto. Kodi tiri monga mwana uja nthawi zina?

Welengani ndime 14 kuti mupeze comwe cinacitika kwa iye. Ataononga ndalama zace, cilala ca njala cinagwa mudziko lija. Cilala citanthauza kuti ndi nyengo ija pomwe mulimi sakhoza kulima cakudya cambiri. Mwina kunalibe mvula yokwanira nthawi ija pomwe mwana uja anali kupeza cakudya sanali kukwaniritsa kucigula. Mnyamata uja anakhala ndi njala pafupi ndi kufa.

Pakumalidza mwana uja anapeza nchito. Anali ndi nchito yakudyetsa nkhumba. Ayuda panthawi ija analibe nazo kanthu nkhumba. Sanali kudya nyama ya nkhumba. Welengani ndime 16 mudzaona cakudya comwe mwana uja anali kudya.

Mndime 17 timauzidwa kuti mnyamata uja "Nzeru zinayamba kubwelelamo m'mutu mwace." Analingalira za kumudzi kwao. Anakumbukira abambo ace. Koma anadziwa kuti comwe anacita cinali coipa. Anakumbukiranso za akapolo omwe Atate alinawo.

Welengani ndime 18-19 mobwezapo. Kodi m'nyamata uja analingalira ciyani? Analingalira za kupita kwa bambo wace. Anali wacisoni kamba ka njira yomwe anacitilamo. Kodi mulingalira kuti anasintha?

Pomwe mnyamata anacoka pamudzi kupita kwina, anakhala ndi nzeru za tsopano. Pomwe analingalira za kubwelera kwa bambo wace sanali cimodzi-modzi. Sanakhulupirire kuti bambo uja azamuitana mwana wace anacimwa. Anali wacisoni kamba ka cimo lace. Koma analibe lingaliro lakuti bambo wace uja azamubvomela kukhala mwana wace. Analingalira za kukafunsa bambo wace kuti iye angakhale kapolo.

BAMBO AKHULULUKIRA

Bambo wace anaona mwana uja pomwe asanafike panyumba. Kodi mulingalira kuti bambo uja anali kuyembekeza kuti mwana wace azabwela?

Bambo wa mwana uja anali wokondwa kwambiri ndi cimwemwe pakuona mwana wace akubwela. Anabvumbatira manja ace kuzungulira thupi la mwana uja. Anamphyophsona mwana uja.

Kodi mwana uja anauza bambo wace ciani? Welengani ndime 21.

Kodi ndi motani bambo uja anasungira mwana wace uja? Welengani ndime 22-24.

Kodi ndi motani momwe bambo anasamalira mwana wace. Anasunga mwana uja monga anali wakufa kale motero kuti waukanso. Ndizobvala zotani zomwe bambo uja anauza kapolo wace kuti abweletse ndi kumveka? Welengani ndime 22.



MUTU 10

## KUKHALA MU LAMULO LA CIKONDI

MAU A MULUNGU: Marko 12:28-34; Luka 10:25-37

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Luka 10:25-37

MAU APAMTIMA:

*Musakhale ndi mangawa kwa munthu ali yense, koma kukondana ndiko; pakuti iye amene akondana ndi mnzace wakwanitsa lamulo.*

*Aroma 13:8*

Kodi mnansi wathu ndani?

Kodi tizawasunga motani anthu ena amene ali kubwalo kwa banja lathu? Yesu anayankha mafunsowa mfanizo limodzi lalikuru pa mafanizo onse. Fanizori likuchedwa "Msamariya wacifundo" werengani nthano kucokera mmau a Mulungu.

*25 Ndipo taonani, wacilamulo wina anaimi-*
*rira namuyesa Iye, nanena, "Mphunzitsi, ndidza-*
*lowa moyo wosatha ndi kucita ciani? 26 Ndipo*
*anati kwa iye, M'cilamulo mulembedwa ciani?*
*Uwerenga bwanji? 27 Ndipo iye anayankha nati,*
*Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako*
*wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu yako*
*yonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mnansi wako*
*monga iwe mwini. 28 Ndipo anati kwa iye, Waya-*
*nkha bwino; cita ici, ndipo udzakhala ndi moyo.*
*29 Koma iye, pofuna kudziyesa yekha wolungama,*
*anati kwa Yesu, Ndipo mnansi wanga ndani? 30*
*Ndipo Yesu anamlanda mau, nati,"Munthu wina*
*anatsika kucokera ku Yerusalemu kunka ku Yeriko;*
*ndipo anagwa m'manja a acifwamba amene anambvula*
*zobvala, namkwapula, nacoka atamsiya wofuna kufa.*
*31 Ndipo kudangotero kuti wansembe wina anatsi-*
*ka njirayo, ndipo pakumuona iye anapita mbali*
*yina. 32 Momwemonso Mlevi, pofika pamenepo,*
*ndi kumuona,iye anapita mbali yina. 33 Koma*
*Msamariya wina ali pa ulendo wace anadza pali*
*iye; ndipo pakumuona, anagwidwa cifundo, 34*

pa nthawi ya masana ndi kuyambata pa nthawi ya usiku. Mwina zinthu zao zikanakhala ndi nguwe. Mmasiku omweo mwina mbala zinali kubwela ndi kuba zonse zomwe anapeza m'masiku omwewo, kulingana ndi masiku ano.

Yesu anauza khamu la anthu lomwe linali kumvela za ulaliki wace kuti asaike mtima ku cuma ca padziko lapansi, popeza zinthu zaozo sizizakhalapo kwa nyengo ya itali. Sanatanthauze kuti munthu sayenera kusunga comwe afuna ai. Anatanthauza kuti ife akristu sitiyenera kusunga cuma cathu kwa ife tokha ai. Anatanthauza kuti ife akristu sitiyenera kusunga cuma cathu kwa ife tokha ai koma kupasako anzathu omwe ali osauka.

Ambuye ali mumtima mwathu, tigwiritsira nchito mbali ya ndalama zathu munjira zace. Motero mbali ya cuma cathu, komweko mtima wathu uzakhala.

ZOLINGALIRA

Nanga inu? Simungakhale ndi ndalama zambiri. Mwina simuzakhala ndi zinthu zambiri. Funso lalikulu ndi iri: Kodi muli wa cuma ndi Mulungu? Kodi mumudziwa monga mphulumutsi? Kodi muli acikondi ndi Mulungu, kapena mumapatsa kwa Mulungu. Kodi pa ndalama yanu mumapereka ndi mtima wanu wonse?

NDEMANGA

1. Cikondwelero coona sicibwera kamba kazinthu zomwe tikhala nazo pa umoyo wathu. Sitipeza cuma coona pa kukhala ndi ndalama.

2. Zinthu zoterezi sizikhala nthawi ya itali pomwe sizinathe. Zingatengedwe kwa ife. Sizizatha kugula Moyo wosatha.

3. Cuma coona cimadza pa kudziwa Mulungu. Cuma cotereci cimabweletsa cikondi, cimwemwe, mtendere ndi moyo wa muyaya.



Bambo anali wokondwa kwambiri pomwe mwana wace anabwela kumudzi komwe kunali bambo wace. Mu ndime 23-24 timaona kuti bambo anacita cinthu cina comwe cinasonyeza kuti, iye anali wokondwa kwambiri. Welengani ndime mobwezapo. Nthawi yomweyo siinali nthawi yokhala m'cisoni ai. Mwana uja anali pa mudzi. Bambo anali wokondwa kwambiri.

Lingalirani za inu eni. Kodi mukanacita cimodzi modzi ngati munali abambo amwanayo?

NTHANO

Yesu ananena nthanoyi kamba ka lingo lina. Anafuna kuti ophunzira adziwe kuti Mulungu akhala okondwa kwambiri ngati munthu yemwe anali otaika tsopano abwela kudziwa Mulungu. Kamba kakuti munthu uja akhala mkuunika tsopano. Anali kufunanso kuti awadziwitse kuti ngati munthu ali ndi macimo ayenera kulapa macimo ace.

KWA INU

Lingalirani za umoyo wanu. Kodi muli ndi cimo lomwe simunafunse Mulungu kuti akukhululukireni? Ngati macimowo muli nawo ndi cifukwa ninji simufuna kufunsa Mulungu kuti akukhululukireni lero lino? M'funseni iye lero lino kuti akuthandizeni kuti mukhale muli kucita cifuniro cace.

NDEMANGA

1. Mwana wa m'ng'ono ali ngati munthu yemwe anena kuti: Sindifuna kukhala m'Kristu. Ndifuna kukhala momwe ndifunira ine mwini.

2. Bambo ali ngati Mulungu. Mulungu adziwa kuti njira zace ndizokoma, koma lekani munthu azisankhire njira yomwe angayendemo.

3. Mulungu akonda ife monga momwe bambo

akondera mwana wace. Ayembekeza ife kuti tifunse kuti macimo anthu akhulululukiridwe. Pomwe tifunsa Mulungu kuti atikhulululukire macimo athu, Mulungu akhala okondwa kucita ici. Apanga ife kukhala ana ace.



cakudya cacing'ono kwa anthu osauka. Kodi anacita ciyani? Welengani ndime 18.

Munthuyu anali wozikonda kwambiri. Munthuyu anali kulingalira za iye mwini coyamba, Motero kuti anali kunyada kwambiri mwa kulingalira kuti moyo uja unali wace cabe.

Welengani ndime 20 muzamva comwe Mulungu ananena. Anacha munthu uja kukhala wopusa. Yesu anagwiritsira nchito mau olimba motero kuti aonetse za kucimwa kwa munthu uja. Wopusa ndi munthu yemwe alingalira za iye mwini. Yesu anamasulira kuti munthuyu sanali kulingalira ponena za Mzimu Woyera. Mu Masalmo 14:1, Davide anacha munthu wopusa, uja yemwe anati kulibe Mulungu. Davide analemba malemba, citanthauza kuti "kulibe Mulungu wanga." Munthu wopusa wotereyu, odziwa kuti Mulungu aliko koma safuna kumutamanda.

Munthu wotereyu mnthano ya Yesu, anaitanidwa kuti opusa. Analibe ndi lingaliro la Mulungu.

Mu ndime 20, kodi Mulungu ananena kuti ndi ciyani comwe cizacitika ku munthuyu? Munthu wolemelayu azafa. Motero ndani amene azatenga mphatso zace?

Yesu anati, munthu aliyense yemwe akonda cuma capadziko lapansi nadana ndi cuma ca Mulungu, munthuyu ndi wopusa.

## CHUMA CA KUMWAMBA

Pa phunziro la pa phiri, Yesu anapereka ziphunzitso zambiri ponena za kukhala ndi cuma kumwamba. Mateyu 6:19-21.

Mtundu wa ciYuda mu masiku aja a Yesu analibe zinthu monga zomwe tilinazo masiku ano. Zobvala cabe ndizo zinali cuma cao. Angakhale masiku ano zobvala ziyenera kusamalidwa. Mbewa zizalowa munkhokwe. Mudziko la Palastini, zobvala zinali kugwiritsidwa nchito kubvala

bambo wao anawasiila kuti atengeko mbali yace.

Yesu sanagwiritsire nchito mphamvu yace munjira yotere. Mundime 14, Ananena cinthu cotere. "Sindinatumidwa kuzagawira cuma anthu. Zinthu zoterezi zizapita. Ndinatumidwa kuzalalikira uthenga, ndi kuthandiza anthu kukhala ndi moyo wa muyaya."

Tsopano welengani ndime 14. Munthuyu ndi wozikonda. Wofuna kuti zonse zizikhala zace. Anali kufuna zonse kukhala za iye yekha. Yesu anagwiritsira nchito cifuniro ca munthuyu ndi ena omwe anali pafupi ndi iye.

Mu ndime 15, Yesu anati, "Musati masiku onse kufuna zinthu zomwe anzanu ali nazo".

Cikhumbo (mundime 15) citanthauza kufuna cinthu cina kamba ka kuti wina yemwe mudziwa ali naco. Citanthauzanso kukhala wozikonda, anafuna zambiri nthawi ndi nthawi. Yesu anauza anthu omwe anali pa khamu la ophunzira kuti ayenera kukhala opewa zikhumbo. Anawauza kuti sayenera kufuna zinthu zomwe ena alinazo.

## MUNTHU YEMWE ANALI WOLEMERA NDI WOPUSA

Yesu analankhula za nthano ya munthu yemwe anali wolemera kwambiri. Welengani nthanoyi mu ndime 16-19. Yanganani za mayankho ku mafunsowa: Ndi mtundu wotani wa munthu amene Yesu analankhula naye? Ndi mutundu wanji wa nchito yomwe inagwiridwa?

Yesu analankhula za munthu wa cuma mu ndime 16. Anali mulimi (Mundime 16-17). Zipatso zace zinali zabwino. Anatenga mbali ya cakudya cace kupatsa anthu osauka? Welengani ndime 16-17 kuti muyankhe mafunso. Kodi anaonga kwa Mulungu kamba ka kupatsidwa mbeu zabwino? Iai. Buku, Lopatulika silimatiuza kuti munthu uja anayamika kwa Mulungu. Sanaperekeko angakhale thandizo kwa anthu osauka. Mu ndime 18 timauzidwa comwe munthu anacita ndi cuma cace. Nkhokwe zace zinali zozala. Sanaperekeko angakhale



MUTU 5

# NJIRA YOMWE MULUNGU APATSIRAMO MPHATSO

MAU A MULUNGU: Mateyu 19:23-20:16

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Mateyu 20:1-16

## MAU APAMTIMA

*Comweco omalidza adzakhala oyamba, ndipo oyamba adzakhala omalidza.*

*Mateyu 20:16*

Mphunziroli tizawelenga za njira yomwe Mulungu anali kupatsiramo mphatso kwa a Kristu. Tsiku lina mnyamata wabwino anadza kwa Ambuye. Anafunsa, "Kodi ndingacite ciyani kuti ndi pulumutsidwe?" Welengani nthano kucokera m'buku la Mateyu 19:16-22. Atacokapo mnyamata uja Yesu anati, "Ndicapatali, kwa munthu wolemela kuti apulumutsidwe." (Mateyu 19:23-26)

Petro anali munthu wosafuna kuti zinthu zimupitire popanda kufunsa, motero iye anati, nanga angapulumuke bwanji iyeyu? Kodi cizatenga ciani?"

Welengani malemba kucokera m'Buku Lopatulika kuti mumve comwe Yesu anayankha, kufunso la Petro.

## MAU A PHUNZIRO

*1 "Pakuti Ufumu wa Kumwamba ufanana ndi munthu mwini banja, amene anaturuka mamawa kuka lembera anchito a m'munda wace wampesa. 2 Ndipo pamene adapangana ndi anchito, pa rupiya latheka limodzi tsiku limodzi, anawatumiza ku munda wace. 3 Ndipo anaturuka dzuwa litakwera, naona ena ataima cabe pabwalo; 4 ndipo kwa iwo anati, "Pitani inunso kumunda, ndipo ndidzakupatsani cimene ciri coyenera." Ndipo iwo anapita. 5 Ndiponso anaturuka usana, ndimonso popendeka*

*dzuwa, nacita cimodzi-modzi. 6 Ndipo poyandi-*
*kira madzulo anaturuka, napeza ena ataima; nane-*
*na kwa iwo, Mwaimiranji kuno dzuwa lonse cabe?*
*7 Iwo ananena kwa iye, Cifukwa palibe munthu*
*anatilemba. Iye anati kwa iwo, Pitani inunso*
*ku mundawo wampesa. 8 Ndipo pamadzulo, mwini*
*munda anati kwa kapitao wace, Kaitane anchito,*
*nuwapatse iwo kulipira kwao, uyambe kwa omarizira*
*kufikira kwa oyamba. 9 Ndipo pamene iwo ole-*
*mbedwa poyandikira madzulo anadza, analandira*
*munthu ali yense rupiya latheka limodzi. 10*
*Ndipo m'mene oyamba anadza, analingalira kuti*
*adzalandira kopambana, ndipo iwonso analandira*
*onse rupiya latheka. 11 Koma m'mene iwo*
*analilandira, anaderera kwa mwini banja, 12*
*nati, Omarizira awa anagwira nchito mphindi*
*yaing'ono, ndipo munawalinganiza ndi ife amene*
*tinapirira kuwawa kwa dzuwa ndi kutentha kwace.*
*13 Koma iye anayankha, nati kwa mmodzi wa iwo,*
*Mnzanga, sindikunyenga iwe; kodi iwe sunapangana*
*ndi ine pa rupiya latheka limodzi? 14 Tenga*
*lako, numuke; pakuti ine ndifuna kupatsa kwa uyu*
*womarizira monga kwa iwe. 15 Sikuloleka kwa*
*ine kodi kucita cimene ndifuna ndi zanga? Kape-*
*na diso lako laipa kodi cifukwa ine ndiri wabwi-*
*no? 16 Comweco omarizira adzakhala oyamba,*
*ndipo oyamba adzakhala omarizira.*

*Mateyu 20:1-16*

## KODI AZAPEDZA CIYANI?

Yesu anadziwa za lingaliro la ophunzira ace anali kulingalira kuti adzakhala wa mkulu ndi ndani? Pa ciyambi sanamvetsetse kuti ufumu wa Yesu unali wakumwamba. Analingalira kuti azakhala oweluza pa dziko lapansi lino. Motero anthu aja anali kufuna mphatso.

Yesu analonjeza ophunzira ace kuti azakhala ndi moyo wosatha. Motero anawauza za nthano ya munda wa mpesa.

## A NCHITO ANALI KUFUNIKA

Mnthano, mulimi anakolola mpesa wace natuta.



*popeza ndiribe mosungiramo zipatso zanga? 18*
*Ndipo anati, Ndidzatere: ndidzapasula nkhokwe*
*zanga, ndi kumanganso zazikuru, ndipo ndidzasu-*
*ngiramo dzinthu zanga zonse, ndi cuma canga.*
*19 Ndipo ndidzati kwa moyo wanga. Moyo iwe,*
*uli naco cuma cambiri cosungika kufikira zaka*
*zambiri; tapumulatu, nudye, numwe, nukondwere."*
*20 Koma Mulungu anati kwa iye, Wopusa iwe,*
*usiku womwe uno udzafunidwa moyo wako; ndipo*
*zinthu zimene unazikonza zidzakhala za yani?*
*21 Atero iye wakudziunjikira cuma mwini yekha*
*wosakhala naco cuma ca kwa Mulungu.*

*19 Musadzikundikire nokha cuma pa dziko*
*lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga;*
*ndi pamene mbala ziboola ndi kuba. 20 koma*
*mudzikundikire nokha cuma m'Mwamba, pamene*
*njenjete kapena dzimbiri sizionongа, ndipo*
*mbala siziboola ndi kuba; 21 pakuti kumene*
*kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso.*

*Luka 12:13-21; Mateyu 6:19-21*

## CIFUNO CA MUNTHU

Yesu anali kuphunzitsa ophunzira ace. Ena anadza kudzamvetsera. Anthu ambiri anasonkhana kubwera kwa Ambuye. Yesu anadziwa kuti analibe nthawi yaikuru ya kuphunzitsa ophunzira ace. Anali kufunika kuti aphunzire zambiri. Motero kuti atafa Yesu iwo angapitilizebe ndi kucita nchito yace.

Welengani kucokera m'Buku Lopatulika, Luka 12:11-12. Yesu anali kuphunzitsa ophunzira ace za zinthu zomwe zikubwela mtsongolo. Anati mudzaimirira pamaso pa oweluza kamba ka kuti mundikhulupirira. Mu ndime 12 timapatsidwa mau acitonthozo; Mzimu Woyera uzakuphunzitsani pa nthawi yomweyo, comwe muyenera kulankhula.

Munthu analankhula kucokera pa khamu la anthu. Welengani mobwezapo Luka 12:13-21. Kodi munthu anafuna kuti Yesu alankhule ciyani? Sitidziwa zambiri za munthu. Munthuyu anali kufuna kuti mbale wace amupatseko cuma comwe

MUTU 9

# KODI CUMA COONA NDI CITI?

MAU A MULUNGU: Mateyu 6:19-34; Luka 12:1-21

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Mateyu 6:19-21; Luka: 12:1-21

MAU APAMTIMA:

*Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu.*

*Mateyu 6:33*

Kodi cuma coona citanthauza ciyani? Kodi citanthauza kukhala ndi ndalama zambiri, mwina galimoto kapena kukhala ndi nyumba yabwino?

Mphunziroli Yesu analankhula za cuma coona. Yesu anati cuma ca kukhala ndi magalimoto, nyumba yabwino kapena ndalama, ici sicuma coona ai. Cuma ndi ici comwe tipedza mtendere ndi mwai wa kukhala ndi moyo wa Muyaya. Ndi kukhala ndi mwai wa kulowa ufumu wa kumwamba.

Welengani ndime kucokera m'Buku Lopatulika. Funa-funani yankho ku mafunso awa, Kodi cuma coona ndi citi?

## MAU A MULUNGU

*13 Ndipo munthu wa m'khamulo anati kwa Iye, Mphunzitsi, uzani mbale wanga agawane ndi ine cuma camasiye. 14 Koma anati kwa iye,"Munthu iwe, ndani anandiika Ine ndikhale woweruza, kapena wakugawira inu?" 15 Ndipo Iye anati kwa iwo,"Yang'anirani, mudzisungire kupewa msiriro uli wonse; cifukwa moyo wace wa munthu sulingana ndi kucuruka kwa zinthu zace ali nazo." 16 Ndipo Iye ananena nao fanizo, kuti, "Munda wace wa munthu mwini cuma unapatsa bwino. 17 Ndipo anaganizaganiza mwa yekha nanena, Ndizatani ine,*



Ngati simukumbukira nthano yace, welengani Buku Lopatulika ndime 1-8 mobwezapo. Mulimi uja anapita kubwalo la msika m'mawa-mawa. Kulingana ndi mwambo wa ciYuda tsiku linali kuyamba pa nthawi ya 6 koloko. Kutanthauzira kuti anali kuyamba zinchito zao pa nthawi yomweyi.

Anchitowa anali ndi cidwi mu kulandira cabe (welengani ndime 2). Anthuwa sanali kupita kunchito kufikira atamva za mtengo wa ndalama coyamba. Ndi zingati zomwe anabvomelezana kuti azasewenzera?

Pa 9 koloko ( pa ola lacitatu) mulimi uja anapitanso ku kafuna anchito ena (ndime 3-4). Anauza anthu kuti azawalipira mtengo womwe uzakhala wabwino kwa iwo. Anakhulupirira iye.

Mulimi uja anali kufunabe anthu kuti akamuthandize ku kolola mpesa. Mu ndime 5 ndi kangati munthuyu wakhala ali kupita kufuna anthu anchito? Anapita panthawi ya masana ndi panthawi ya kumadzulo pa 3 koloko pa ulendo wotsiriza anapita ndi nthawi ya 5 koloko, Mulimi uja anabwelela kukabweletsa anthu ambiri. Pomwe anaona kuti anthu aja sanali kugwira nchito, anafunsa, mu mau alero "Kodi ndicifukwa ninji simugwira nchito?" (Welengani ndime 6) Motero anauza anthu aja kuti apite kukagwira nchito m'munda wa mpesa. Sanafunse za malipiro.

## MPHATSO

Welengani mu ndime 8-12 mobwezapo motero kuti mumve njira yomwe analipiliramo anthuwa.

Pomwe nthawi ya m'madzulo inafika, mulimi uja mwini munda anauza Kapitao kuti ayambe kulipira aja omwe abwela nthawi ya masana, omwe anali osirizira kulembedwa nchito. Anatsirizira ndi anthu omwe anayambira coyamba.

Kapitao anapatsa anthu aja omwe anasalira kulembedwa, ndalama ya siliva imodzi. Iyi kundalama ya tsopano monga ya kuno kwathu ndi 10 ngwee. Iyi inali ndalama yomwe munthu anali

kulipilidwa, kamba ka kugwira nchito yace yatsiku, monga kumatsiku aja aumoyo wa Yesu. Anthu omwe sanagwire nchito yao kucokera m'mawa kufikira m'madzulo, anangolandira 10 ngwee. Anali okondwa kwambiri.

Motero kapitao anapereka malipiro awo kwa aja omwe anayamba kugwira nchito pa nthawi ya m'mawa. Anabvomera kuti azasewenzera 10 ngwee. Welengani 11-12 muzamva comwe anthu aja adanena.

Anthu aja omwe anayambira kulipilidwa anacita kaduka monga ana ang'ono. Mulimi anali ngati Mulungu. Anasunga a nchito ace cimodzimodzi. Anati,"sindinakunameni inu. Mwanena kuti muzasewenzera ndalama ya Siliva inu eni." (ndime 13)

Welengani ndime 14-15 mobwezapo. Mulimi uja anafuhsa mafunso awiri omwe tiyenera kufunsa lero lino: "Ndilibe mphamvu ya kugwiritsira nchito ndalama mnjira yosayenera? Kodi mwakhala ndi kaduka kamba kakuti ndimalipira mwa ufulu?

Mundime ija ya 16 Yesu anauza Petro "Iwo omwe obwela kale sanadandaule za malipiro awo kapena phatso zomwe aja oyamba azalandira. Iwo omwe obwela paciyambi ndi kuti anali odandaula kamba ka malipiro azapatsidwa mphatso potsiliza. Kukhala ndi kaduka ndi colakwa. Palibe munthu yemwe ayenera kumva kuti ali oposa wina

Kodi mufuna kutamandidwa pa nchito ili yonse yomwe mugwira pa nyumba kapena ku Chalichi?

Sabata lino pomwe mugwira nchito ya Ambuye, khalani cete musauze munthu aliyense kuti ndinu mwacita nchitoyi.

NDEMANGA

1. Mkristu ayenera kugwira nchito ya Mulungu kamba kakuti amukonda, Palibe yemwe angalire za kulipilidwa, kapena kutamandidwa, kamba ka zocita zace za bwino.



lingaliro mwa cifuniro cao kuti cikhale copewelako.

2. Anthu ambiri amanena kuti akonda Mulungu, koma moyo wao siuonetsa kuti amukonda iye. Alemekeza Mulungu ndi pakamwa pao. Samulemekeza iye mu umoyo wao.

3. Ngati munthu adziwa za cifuniro ca Mulungu ndi kuti sacitsatira, sangakhale ndi cikhulupiriro mwa Mulungu.

nkha mokomeza bambo wace. Anaitana bambo wace "Atate" ndizapita kukagwira nchito koma pambuyo pace mwana uja sanapite kukagwira nchito.

Mundime 31 Yesu anafunsa akuru funso. Kodi ndifunso lotani lomwe anawafunsa? Anawafunsa kuti achule mwana yemwe anacita cifuniro ca Atate wace, comwe anawauza kuti acite. "Mwana wa mkuru," anayankha motero. Welengani comwe Yesu anawauza.

Ayuda anali kudana ndi anthu a msonkho, ndi anthu acigololo. Koma Yesu anawauza kuti koma anthuwa azalowa ufumu wa kumwamba kuposa alaliki ena ndi atsogoleri awo. Ndi cifukwa ninji anatero Yesu? Pezani yankho mundime 32.

Atsogoleri azipembezo anali ngati mwana uja wa ciwiri. Amanena kuti akonda Mulungu. Amamucha iwo bambo, koma sacita za cifuniro cace.

Yesu anawauza kuti coyamba yohane mbatizi anawauza za njira yabwino. Koma sakanakhulupirira iye. Yesu anati, "angakhale pomwe munaona ici (amisonkho ndi azigololo ali kukhulupirira mu uKristu) simunasinthe nzeru zanu coyamba ndi kuti mukhulupirire mwa iye." (ndime 32)

Anthu amisonkho ndi anthu azigololo anali anthu ocimwa kwambiri. Pomwe anamva Yohane m'Batizi, ndi kuzamvanso kwa Yesu, anakhala acisoni kamba ka macimo awo. Anakhulupirira mu zomwe anamvela. Anasintha malingaliro awo oipa. Anakhulupirira nacita comwe Mulungu anawauza kuti ayenera ku mutsatira.

NDEMANGA

1. Buku Lopatulika limati tiyenera kudziwa ndi kucita cifuniro ca Mulungu. AKristu ambiri anadziwa ndi kucita cifuniro ca Mulungu. Akristu ambiri adziwa comwe Mulungu afuna. Amanena iwo eni kuti, sindifuna kucita ici," mwina anapanga



2. Ngati alipo omwe tigwira nawo nchito, ndi kuti alikusungidwa bwino, sitiyenera kukhala ndi kaduka naye, koma tiyenera kukhala okondwa. Palibe m'Kristu yemwe ayenera kukhala ndi kaduka kamba kakuti zabwino za bwela ku anzao.

3. Tiyeni tikhale oyamika kuti Mulungu sazapatsa mphatso molingana ndi nchito zomwe ticita kwa iye. Mulungu ali wacifundo aza dalitsa ife tonse koposa.

MUTU 6

# KUPITILIRA M'PEMPHERO

**MAU A MULUNTU:** Luka 11:5-13; 18:1-8

**MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO:**
Luka 11:11-13 Luka 18:1-8

**MAU APAMTIMA**

*Pakuti aliyense wakupempha alandira; ndi wofunayo apeza; ndi iye amene agogoda adzatsegulira.*

*Luka 11:10*

Kupitiliza citanthauza kuti kupitilizabe kucita cinthu cimodzi ndi cimodzi. Mphunziro ili tiwelenga za kufuna kwa kupitirizabe kupemphera.

Tsiku lina Yesu anali kupemphera. Anali kupemphera nthawi ndi nthawi. Patsikuli ophunzira anafunsa, "Ambuye tiphunzitseni kupemphera, monga momwe Yohane anaphunzitsira ophunzira ace." (Luka 11:1)

Luka 11:24 timapatsidwa mau amapemphero, kapena pemphero la Ambuye, monga momwe timaitanira.

Yesu anauza ophunzira ace nthano ya kukhalabe muli kupemphera monga momwe tingakhalire tiri kupemphera. Patapita kanthawi anawapatsanso nthano yotanthauza cimodzi-modzi. Welengani nthano ziwiri.

*11 Ndipo ndani wa inu ali atate, mwana wace akadzampempha mkate, adzampatsa mwala? Kapena nsomba, nadzamninkha njoka m'malo mwa nsomba? 12 kapena akadzampempha dzira kodi adzampatsa cinkhanira? 13 Potero, ngati inu, okhala oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, koposa kotani nanga Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo*



amanga nyumba yace pa m'cenga.

Mbali mwa mtsinje womwe unali ndi madzi ambiri, munthuyu anati awa ndiwo malo omwe ndingamangepo nyumba yanga. Mnyengo ina ya nthawi munali kudzala madzi m'kati muja. Mwina anthu ena anamanga manyumba yao pa m'cenga. Motero pomwe mvula inagwa manyumba onse anagwa.

Nthawi zina anthu mumiyoyo yao amakhala ngati anthu aja omwe anamanga manyumba yao pa mcenga. Akhala alibe maziko. Adziwa kuti ayenera kulandira Ambuye. Aziwa kuti ayenera kucita cifuniro cace. Anthuwa alingalira za kukhala opanda Ambuye. Pomwe imfa ibwela, akumbukira za kulakwa kwao. Ici cimacitika pomwe zinthu zapita kale.

ANA AWIRI

Tsiku lina atsogoleri azipembezo anadza kwa Yesu namfunsa iye "Ndani anakupatsa mphamvu ya kucita zinthuzi zomwe ukucitazi?" Welengani kucokera m'Buku Lopatulika, Mateyu 21:24-27 muzapedza yankho lomwe Yesu anawapatsa. Motero anauza anthu zanthano. Welengani Mateyu 21:28-32.

Mlimi wina anali ndi ana awiri. Mpesa wace unali utaphya (kutanthauza kuti inafika nthawi yakukolola.) Bambo uja anafunsa mwana wace wa mkulu uja kuti apite kukagwira nchito kumunda. Welengani ndime 29 ndi kuyankha mafunsowa: Kodi mwana wa mkuru uja anati bwanji? Kodi mwana uja anapita kukagwira nchito? Mwana uja anali anakana paciyambi kuti safuna kupita kukagwirira nchito bambo wace, koma patapita kanthawi mwana uja anazindikira kuti pa kukanira bambo wace, kunali kulakwa, motero mwana uja anapita kukagwira nchito kumunda.

Mlimi uja anafunsa mwana wace wa ciwiri kuti apite ku kagwira nchito ku munda wa mpesa, Kodi ndimezo ngati tawelenga zimatiuza bwanji ponena za mwana wa ciwiri uja? Welengani mobwezapo. Muzamva comwe mwana waciwiriyu anaya-

patsiku la ciweluzo Yesu azabwela kuzatiweluza ife. Anthu azauza Yesu kuti iwo ali abwino pomwe adzabwela kuza tiweluza ife. Anthu ambiri azauza Yesu kuti iwo ali abwino. Welengani ndime 23 muzamva comwe Yesu anena kwa iwo.

Mu ndime 24-25, Yesu anawauza zamunthu yemwe amvera zomwe analankhula. Kuti iyeyu akhala ngati munthu yemwe amanga nyumba yace patanthwe.

## KUMANGA PATANTHWE

Pomwe wina afuna kumanga nyumba yabwino, ndi yamphamvu, coyamba azakumba pansi naika maziko ace a sementi. Pomwe nyumba izatha mphepo ya namodwe ina omba, Koma nyumba siizagwedezeka. Ndiyomangidwa pa maziko a tanthwe.

Cikhulupiriro mwa Ambuye Yesu ndi kumanga nyumba yace pa "tanthwe". Ici citithandiza ife kukhala aKristu oona. Cikhulupiriro citanthauza kukhala olimba mu nthawi ya mabvuto.

Ngati munthu acita cabwino pomwe mzace amucitira coipa, timati munthuyu ali ndi maziko abwino.

Pomwe mtsikana kapena m'nyamata, ali kutumikira Mulungu angakhale ali pa ulendo, kapena ali ku mbali kwina kwace, timati munthuyu amanga nyumba yace patanthwe.

Ngati munthu akhulupirira mwa Ambuye angakhale panthawi ya mabvuto monga ya imfa kapena matenda, timati munthuyu amanga nyumba yace pa tanthwe.

## MUNTHU WOPUSA

Welengani ndime 26-27 mobwezapo ndi cifukwa ninji Yesu anaitana munthu wina kukhala wopusa? Yesu anati munthu yemwe samvera za kalankhulidwe ka Yesu, ali ngati munthu yemwe



*akumpempha Iye?*

*Ndipo anawanenera fanizo lakuti ayenera iwo kupemphera nthawi zonse, osafoka mtima; 2 nanena, M'mudzi mwakuti munali woweruza wosaopa Mulungu, ndi wosasamala munthu. 3 Ndipo m'mudzimo munali mkazi wamasiye; ndipo anadza kwa iye nanena, Mundiweruzire mlandu pa wotsutsana nane. 4 Ndipo sanafuna nthawi; koma bwino bwino anati mwa yekha, Ndingakhale sindiopa Mulungu kapena kusamala munthu; 5 koma cifukwa ca kundibvuta ine mkazi wamasiye amene ndidzamweruzira mlandu, kuti angandilemetse ndi kudzaidza kwace. 6 Ndipo Ambuye anati Tamverani conena woweruza wosalungama. 7 Ndipo kodi Mulungu sadzacitira cilungamo osankhidwa ace akumuitana usana ndi usiku, popeza aleza nao mtima? 8 Ndinena ndi inu, adzawacitira cilungamo posacedwa. Koma Mwana wa munthu pakudza Iye, adzapeza cikhulupiriro pa dziko lapansi kodi?*

*Luka 11:11-13; Luka 18:1-8*

Kucokera m'Buku Lopatulika, welengani Luka 11:5-10. Yesu analankhula za munthu yemwe anali kugogoda pa khomo labwenzi lace pa nthawi ya usiku.

Munthu wogona uja anamva za kugogoda. Motero anamva za mbale wace yemwe anali kunena kuti "Tsegulani khomo. Ndipatseni mkate. Kwabwela munthu yemwe wabwela kundicezela. Ndiyenera kumupatsa cakudya." "Pita uko," anatero mwamuna uja. "Uzandiutsira ana anga." Koma bwenzi wace uja sanapite. Kufikira munthu uja yemwe anali mnyumba anaima natenga mkhate ndi kutsegula kukhomo napatsa wogogodayo mkhate, namuyanganira ali kuyenda kubwelela kunyumba yace.

Kodi Mulungu ayankha pemphero lathu kamba

kakuti watopa nafe, ndi kuti afuna kuti tisiye kumupempha? Welengani Luka 11:9-10. Yesu anauza ophunzira kuti akhalebe ali kupemphera. Mulungu sali ngati munthu uja. Mulungu akonda ife. Afuna kuyankha mapemphero athu.

Mwina Mulungu sangatipatse comwe tifuna kupempha. Tili ndi macimo mumoyo wathu. Sititumikira Mulungu munjira yomwe tiyenera. Tifunsa zinthu zomwe ziri zoipa. Ambuye afuna kufunsidwa zinthu zomwe zingathandize inu kukhala mKristu wabwino.

Mwina sitikhala ndi cikhulupiriro. Pomwe Mulungu sayankha pemphero lathu pomwepo, timasiya ku pemphera. Ambuye afuna ife kupitilizabe kupemphera, kuti cifuniro cace cingacitike kwa ife m'moyo wathu.

## MULUNGU APATSA MPHATSO ZABWINO.

Tsopano welengani Luka 11:11-13. Azibambo aci Yuda anakonda ana awo. Anali kuwasamalira. Yesu anadziwa kuti ophunzira ace azamvetsetsa za zomwe bambo wa bwino amacita. Kodi bambo wa uja azapatsa mwana wace zinthu monga za lembedwa mum'ndandanda yace, mu ndime 12?

Mu ndime ya 13 Yesu analankhula m'mau athu alero, "Muli ngati Mulungu. Ngakhale ana anu ndi olakwa, koma mukali kuakondabe. Muwapatsa zinthu zabwino. Koma bambo wanu aliwoposa. Ndi cacilengedwe kuti iye apatsa Mzimu Woyera ku ana ace."

Yesu anadziwa kuti Mzimu Woyera unali wabwino koposa mphatso zonse. Palibe mphatso ina yomwe ingabweretse mtendere kwa munthu. Palibe angakhale mphatso yomwe ingapangitse munthu kukhala ndi mtendere wabwino.

## KUWELUZA KOIPA

Tsopano welengani Luka 18:1-8 mobwezapo. Kodi ndicifukwa ninji Yesu ananena nthanoyi? Welengani ndime 1. Yesu anali kufuna kusunga



*zinaomba mphepo, zinagunda pa nyumbayo; koma*
*siinagwa; cifukwa inakhazikika pathanthwepo.*
*26 Ndipo yense akamva mau anga amenewa, ndi*
*kusawacita, adzafanizidwa ndi munthu wopusa,*
*yemwe anamanga nyumba yace pamcenga; 27 ndipo*
*inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba*
*mphepo, zinagunda pa nyumbayo; ndipo inagwa;*
*ndi kugwa kwace kunali kwakukuru. 28 Ndipo*
*panakhala pamene Yesu anatha mau amenewa,*
*makamu a anthu anazizwa ndi ciphunzitso cace:*
*29 Pakuti anawaphunzitsa monga mwini mphamvu,*
*wosanga alembi ao.*

*28 Nanga mutani? Munthu anali nao ana*
*awiri; nadza iye kwa woyamba nati, Mwanawe,*
*kagwire lero nchito ku munda wampesa. 29 Koma*
*iye anakana, nati, Sindifuna ine; koma pambuyo*
*pace analapa mtima napita. 30 Ndipo anadza*
*kwa winayo, natero momwemo. Ndipo iye anabvo-*
*mela, nati, Ndipita mbuye; koma sanapita. 31*
*Ndani wa awiriwo anacita cifuniro ca atae wace?*
*Iwo ananena, kwa iwo, Indetu ndinena kwa inu,*
*kuti amisonkho ndi akazi aciwerewere amatsogo-*
*lera inu, kulowa mu Ufumu wa Kumwamba. 32*
*Popeza Yohane anadza kwa inu m'njira ya cilunga-*
*mo, ndipo simunamvera iye; koma amisonkho ndi*
*akazi aciwerewere anammvera iye; ndipo inu,*
*m'mene munaciona, simunalapa pambuyo pace, kuti*
*mumvere iye.*

*Mateyu 7:21-29; 21:28-32*

## KUMVA NDI KUCITA

Mu ndime 21 timapatsidwa coonadi comwe tifuna tsopano. Ndimeyi imati siyense azapita kumwamba. Kodi mudziwa kuti ngati munthu ndi mKristu, ayenera kukhala monga mkristu?

Mmau alero, Yesu anati, "Munthu aliyense yemwe azanena kuti ndine mkristu, iyeyu sindiye. Munthu azacha ine Ambuye koma angakhale kutero sazalowa mu ufumu wa kumwamba." Mayeso omwe ayenera kupambana ndi a kumvera Mulungu.

"Mutsiku lija" (Ndime 22) itanthauzira

MUTU 8

# KUDZIWA NDI KUCITA CIFUNIRO CA MULUNGU

MAU A MULUNGU: Mateyu 7:21-29; 21:23-32

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Mateyu 7:21-27; 21:28-32

MAU APAMTIMA:

*Siyense wakunena kwa ine Ambuye, Ambuye, adzalowa ufumu wa kumwamba; koma wa cita cifuniro ca Atate wanga wa kumwamba adzalowa.*

*Mateyu 7:21*

Cifuniro ca Mulungu citanthauza comwe Mulungu afuna ife kuti ticite. Mulungu ndi Atate wathu wakumwamba. Ali ndi nzeru za pa munthu aliyense.

Mphunziroli tizaphunzira za cifuniro ca Mulungu ndi momwe tingacigwiritsire nchito.

Ndime yathu kucokera m'Buku Lopatulika muli nthano ziwiri zomwe Yesu analankhula. Welengani ndime ziwirizo kucokera m'Buku Lopatulika.

MAU A MULUNGU

*21 Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye,*
*Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba. 22*
*Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye,*
*Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi*
*m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi*
*kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? 23*
*Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudzi*
*wani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu*
*akucita kusayeruzika. 24 Cifukwa cimeneci*
*yense amene akamva mau anga amenewa, ndi kuwa-*
*cita, ndidzamfanizira iye ndi munthu wocenjera,*
*amene anamanga nyumba yace pathanthwe; 25*
*ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo*



ophunzira ace kuti azipemphera tsiku ndi tsiku. Anadziwa kuti sazakhala ali kukomana ndi zabwino zokhazokha ai. Azaperekedwa kamba ka kutsatira iye. Motero anafuna iye kuti akumbukire za nthano yace. Sanafune iwo kuti azikhala ndi mantha.

Unali mtundu wotani wa oweluza yemwe Yesu anafanizira munthano yace? Kodi ndizinthu ziwiri zotani zomwe ndime 2 imanena za munthuyu?

Kodi mwapeza kuti oweluza uja sanaope Mulungu? Oweluza mwina anali kulakwa mwina anali kutsatira zabwino. Alibe angakhale lingaliro la bwino. Lingaliro la kudziwa cabwino ndi coipa comwe tikhala naco. Lingaliro lomwe tikhala nalo ndi lakuphunzitsidwa. Ngati mudziwa cabwino ndi coipa motero lingaliro la kucita zabwino likhala-po. Oweluza sakhala ndi zeru za kuphunzitsidwa colinga cabwino kapena coipa.

Kodi mwapedza kuti oweluza sanalemekeze anthu? Oweluza anali kulingalira za iye yekha. Ngati munthu ali pafupi ndi nyumba yanu yemwe ali ndi mabvuto, siciwawa iye. Uyu ngati anali ndi mpata wa kunama munthu iye ankanacita tero.

Mzimai wamasiye wa mmudzi anapita kwa oweluza kuti akadandaule za mwamuna yemwe anapweteka mkaziyo. (Mundime ya citatu 3).

Oweluza anadziwa kuti anali kunamizidwa. Sanali kumuthandiza. Welengani ndime 4-5 mobwezapo. Kodi mkazi uja anasiya kukambisana ndi oweluza? Iai. Anadziwa kuti oweluza uja ndiye yekha yemwe angathe kuthandiza.

Oweluza anati kwa iye mwini sindiopa Mulungu ndi kutinso sindilemekeza munthu. Koma mzimaiyu ali kundibvuta kwambiri ndi mabvuto ace. Motero ndizathandiza, maiyu motero kuti asandibvutenso ine.

Kodi bvutoli litanthauzira ciyani? Yesu anati ngati oweluza woipa uja anathandiza mzimai uja yemwe anali ku khalabe ali kufunsa thandizo.

Kodi Bambo wathu wa kumwamba azathandiza ana ace omwe iye akonda?

Mndime 7-8, Yesu anauza ophunzira kuti Mulungu azathandiza anthu ace. Mulungu sayankha mapemphero athu nthawi zonse pomwe tipemphera. Tiyenera kukhala ndi cikhulupiriro coyamba, ca kuti Mulungu azayankha mapemphero athu akutinthandiza kuti tikhale olimba pa kucita nchito yace.

## ZA KUGANIZIRA

Yesu anali kupemphera tsiku ndi tsiku. Ngati mwana wa Mulungu anali kupemphera, lingalirani ndi kangati akristu ayenera kupemphera? Tiyenera kufuna kuti tikhale odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Mzimu Woyera utithandiza ife kuti tizikhala monga a Kristu mu umoyo wathu. Tiyenera kufunsa ndi cisomo. Cisomo citithandiza ife ngati tagwa m'mabvuto, matenda, ndi imfa. Cikhulupiriro cithandiza ife kuuzako anzathu za Mau a Mulungu.

Ngati tipemphera modekha mtima pa zinthuzi, Mulungu azatidalitsa mu zinthu zambiri.

## NDEMANGA

1. Mulungu akonda ife. Sali ngati munthu uja yemwe sapatsa mkhate kumnzace wapempha, kapena monga oweluza oipa uja.

2. Mulungu afuna kuti atipatse zinthu zabwino, ngakhale Mzimu Woyera. Azatisamalira ife kuposa bambo wathu wa padziko lapansi.

3. Mulungu azafuna ife kukhalabe tiri kupemphera nthawi ndi nthawi. Tiyenera kukhulupirira Mulungu kuti adzayankha mapemphero athu. Sayankha pa nthawi imodzi. Adzakuyankhani munjira yabwino ndi nthawi yabwino.



Mu ndime yotsiriza ya 14, Yesu analankhula za ufumu wa Mulungu. Anthu ozikonda azacepetsedwa. Anthu ozicepetsa azakuzidwa.

## NDEMANGA

1. Yesu afuna ife kukhala ozicepetsa. Afuna ife kuti tisalingalire zambiri ponena za ife eni.

2. Ife a Kristu tiyenera kulinganiza za umoyo wathu ndi umoyo wa Yesu Kristu. Sitiyenera kulinganiza umoyo wathu ndi anthu ena.

awiri. Pemphero la munthu wa mtundu wa Afarisi linali pemphero lalitari kwambiri. Pemphero la munthu wa msonkho linali lalifupi. Anthu awiriwa sanalingalire molingana ai. Kodi mfarisi anali munthu wotani? Kodi anali wabwino? Anali wozikuza? Wozikonda? Wosakhulupirika? Wabwino? Mfarisi analibe lingo la kufuna Mulungu. Anaganizira kuti anali wabwino payekha angakhale popanda Ambuye.

WABWINO KUPOSA MUNTHU UJA?

Kasano ndi kamodzi Mfarisi anakhala ali kuchula zina lace. Ndizinthu zotani zina zomwe anayamika kwa Mulungu? Anatamanda Mulungu kamba ka kuti iye sanali ngati munthu wina. Mfarisi analingalira kuti iye anali wabwino kuposa anthu onse. Anatamanda Mulungu kamba ka kuti iye sanali monga munthu wa m'sonkho uja. Anali kuona macimo a ena. Iye sanaone macimo ace. Mulibe za umunthu m'pemphero la Mfarisi uja. Ndi yani yemwe ananena pemphero lace? Pezani yankho mundime ya 11.

Yesu apa anati "Mfarisi uja anali kulankhula pemphero lija kwa iye yekha" Yesu anatanthauza kuti Mulungu sanamve pemphero la munthu uja. Yanganani ku munthu wa msonkho sanali wozikuza ai. Anaima payekha. Anaika mutu wace pansi. Anali ndi mantha a kuyangana kumwamba. Sanalankhulapo za kukoma kwace. Anadziwa kuti munthu uja anali ocimwa. Munthu wa msonkho uja anali wacisoni kamba ka macimo ace. Anafunsa Mulungu kuti amumvele cifundo. Welengani za pemphero lace la lifupi kucokera mundime 13.

Ndiciyani comwe anafunsa Mulungu kuti amuthandize? Anafunsa za cifundo ca Mulungu. Anaitana iye mwini kukhala wocimwa.

Munthu wa m'sonkho anadziwa kuti anali wocimwa. Anafunsa cikhulukiro. Kodi Mulungu anali kumvela za pemphero lace? Welengani ndime 14.



MUTU 7

# UMUNTHU PAMASO PA MULUNGU

MAU A MULUNGU: Luka 14:7-11, 18:9-14

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO:
Luka 14:7-11; Luka 18:9-14

MAU APAMTIMA:

*Cifukwa munthu aliyense wa kuzikuza adzacepetsedwa.*

*Luka 14:11*

UMUNTHU citanthauza kukhala wosazikonda iwe mwini. Munthu yemwe adziwa za umunthu sayenera kulingalira kuti iye ali wopambana ena. "Umunthu pa maso a Mulungu" citanthauza kuonetsa Mzimu Woyenera pamaso pa Mulungu. Munthu yemwe aonetsa mzimu wabwino pa maso pa Mulungu, ndi uja yemwe akhala wozicepetsa. Salingalira kuti iye ali wabwino kupambana ena popanda Mulungu. Adziwa kuti afuna Mulungu.

Luka 14:1-6, timawelenga kuti Yesu anadya cakudya mnyumba ya "mkuru" wa Afarisi. Yesu anali kuyangana anthu omwe anali kupedzeka pa phwando paja. Anaona kuti anthu aja anali kufuna phunziro. Welengani ndime. Ndiphunziro lanji lomwe Afarisi anali kufuna ku phunzira?

MAU A MULUNGU

*7 Ndipo Iye ananena fanizo kwa oitanidwa, popenya kuti amadzisankhira mipando yaulemu, nanena kwa iwo, 8 Pamene pali ponse waitanidwa iwe ndi munthu ku cakudya ca ukwati , usaseama pa mpando waulemu; kuti kapena wina waulemu wakuposa iwe akaitanidwe ndi iye, 9 ndipo pakufika iye amene adaitana iwe ndi uyu, adzati kwa iwe, Mpatse uyu malo; ndipo pomwepo udzayamba manyazi kukhala pa mpando wa kuthungo. 10 Koma pamene pali ponse waitanidwa iwe, pita nukhale pansi pa malo a kuthungo; kotero kuti*

*pamene akadza iye anakuitana iwe, akanena ndi iwe, Bwenzi langa, sendera, kwera kuno; pomwepo udzakhala ndi ulemerero pamaso pa onse akusea-ma pacakudya pamodzi ndi iwe. 11 Cifukwa munthu ali yense wakudzikuza adzacepetsedwa; ndipo wakudzicepetsa adzakulitsidwa.*

*Ndipo anatinso kwa ena amene anadzikhulu-pirira mwa iwo okha kuti ali olungama, napepu-tsa onse ena, fanizo ili, 10 Anthu awiri anakwera kunka kukacisi kukapemphera; winayo Mfarisi ndi mnzace wamsonkho. 11 Mfarisiyo anaimirira napemphera izi mwa yekha, Mulungu, ndikuyamikani kuti sindiri monga anthu onse ena, opambapamba, osalungama, acigololo, kapenanso monga wamsonkho uyu; 12 ndisala cakudya kawiri sabata limodzi; ndipereka limodzi la magawo khumi la zonse ndiri nazo. 13 Koma wamsonkhoyo alikuima patali sanafuna kungakhale kukweza maso kumwamba, komatu ana-dziguguda pacifuwa pace nanena, Mulungu mundicitire cifundo, ine wocimwa. 14 Ndinena ndi inu, anatsikira kunyumba kwace woyesedwa wolungama uyutu, wosati uja ai; pakuti yense wakudzikuza yekha adzacepetsedwa; koma wodzi-cepetsa yekha adzakulitsidwa.*

*Luka 14:7-11; Luka 18:9-14*

## MALO ABWINO OKHALAPO

Yesu anaona kuti kunali anthu ena omwe anali kufuna kukhala pa malo abwino. Anaona kuti oitanidwa aja anali ozikonda kwambiri. Kodi Yesu anawauza ciani mundime 7? Yesu anawauza kuti asazikhala m'mipando yabwino. Kodi ananena ici kamba ka ciyani? Welengani ndime 8-9.

Kodi mwapeza kuti Yesu ananena kuti, "mwa oitanidwa akuru a zabwela wina wolemeke-zeka? Kwa iwo omwe anasankha m'malo abwino, mwina azayamba ku cotsedwa? Yesu anawauza kuti powacotsa azakhala ndi manyazi pomwe anzao azayamba kuayangana ali kusintha malo awo nakhala pamalo ena.



Mundime 10, Yesu anawuza za njira yabwino. Mmau alero, anati, "Ndi cabwino kukhala pa mpando woipa coyamba." Ogawa cakudya mwina anga kuitaneni kukakhala pa mpando wabwino. Anzanu azaona inu muli kuyenda, kucoka pa malo oipa kunka patsopano. Azalingalira kuti muli olemekezeka, (ochuka) koma osati munthu wozikonda.

## KUKHALA OCHUKA KOMA OSAZIKUZA

Ndidziwa mzimai yemwe ali wochuka koma sali wozikuza kapena ku nyada. Analemba mabuku ambiri mbiri. Ali kuphunzitsa pa Sukulu ya kuya (Univesiti). Ndi mai wa udongo kwambiri. Koma maiyu sali wonyada. Nthawi zina amafunsidwa kukhala pa malo ouma, maiyu amangokhala popanda kuonetsa kunyada konse. Anzace amati, "Mai uja sadziwa kuti iye ali wochuka kwambiri."

Ali ndi Umunthu wabwino. Yesu Kristu anali ndi umunthu. Munthu wofasa saganiza kuti iye ali wabwino kuposa ena.

## ANTHU AWIRI ANALI KUPEMPHERA

Yesu ananena za nthano ina ponena za Umunthu. Welengani mobwezapo Buku la Luka 18:9-14.

Pezani mayankho ku mafunsowa:

1. Ndi anthu angati omwe anapita ku kacisi? (Welengani ndime 10)
2. Kodi anthuwa anali otani? (Ndime 10)
3. Kodi dzina lina la wa msonkho ndiliti? (Munthu wa msonkho yemwe anali kugwira nchito mu ulamuliro wa ci Roma).

   Ayuda anali kudana ndi anthu a msonkho.

Mndime 11:13 imatipatsa pemphero la anthu